

ZITSIME ZONG'ALUKA



Tiyeni ife tipemphere. Ambuye, tsopano ife tikukhulupirira. Ife tikukhulupirira pa Mwana wa Mulungu, ndipo, kupyolera mu ichi, ife tikulandira Moyo Wamuyaya kupyolera mwa Iye. Tsopano ife tasonkhana kanonso, madzulo ano, kapena usiku uno, kwa msonkhano wina, kudalira Inu pa Uthenga ndi pa chimene Inu muti mutiwuze ife usikuuno. Ife tikukhulupirirani Inu, Ambuye, ndipo ife tikuyembekezera pa Inu. Ndipo Inu munati, “Iwo amene ayembekezera pa Ambuye adzawonjezera mphamvu zawo; iwo adzakwera mmwamba ndi mapiko monga mphungu.” Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu mudzatipatse ife Mphamvu iyo yokwerera-mmwamba, usikuuno, pamene ife tikuyembekezera pa Inu.

² Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha anthu awa, ndi pa chimene iwo akutanthauza kwa Inu ndi chimene iwo akutanthauza kwa ine. Ine ndikukuthokozani Inu chifukwa cha icho, Atate. Iwo ali ngale Zanu. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti usikuuno, kuti Inu mudzadziwonetsera Nokha mwa njira, kwa iwo, imene iwo ali nako kusowa kwake. Ngati pali odwala pano, mulole iwo kuti achiritsidwe. Ngati pali kukayika mu malingaliro a winawake; kuchotseni iko umu, Ambuye. Ndipo ingotipatsani ife za Kukhalapo Kwanu ndi madalitso Anu, chifukwa ife tikuwasowa iwo, Ambuye. Inu ndinu wokwaniritsa-zonse wathu. Ndipo, popanda Inu, ife sitingakhoze kuchita kalikonse.

³ Ife tikupemphera kuti Inu mulandire mathokozo athu operekedwa chifukwa cha zonse zimene Inu mwazichita. Mu Dzina la Yesu Khristu ife tikuyang'anira ku madalitso Anu. Amen.

Inu mukhoza kukhala.

⁴ Ndipo, chabwino, izo zangokhala—mwazizirira pang'ono usiku wa Lamlungu uwu, mkati muno, kuposa momwe izo zinaliri usiku wa Lamlungu watha. Ndife oyamikira kwambiri kwa abale athu amene anagwira ntchito mokhulupirika chotero kuti alowetse izi muno. Ine ndikuwadziwa awiri kapena atatu a iwo. M'bale Mike Egan, monga ine ndikumuwona kumbuyo uko, ndi ine . . . M'bale Mike, ndi M'bale Sothmann, M'bale (ine ndikukhulupirira) Roy Roberson, ndi M'bale Woods, ndi onse a iwo, iwo anabwera kuno kudzakhetsera thukuta basi pa izi, kuyesera kuti azilowetse izo mkati kotero kuti ife tikanakhoza kukhala nawo Uthenga uwu tsopano, kapena lero. Kotero, ndife oyamikira.

⁵ Tsopano, Lamlungu likubwerali mmawa, Ambuye akalola, ine ndikufuna kuti ndikhale ndi msonkhano wamachiritso,

mapemphero a pa odwala. Ndipo ife tidzawukonza iwo kuti ukhale msonkhano wa machiritso, ngati Ambuye alola.

⁶ Ine ndinazindikira, mmawa uno, pali mulu wa mipango apa. Ine ndinayipempherera iyo. Ndipo ine, pamene inu munali kupemphera ndi kuyimba, ine ndinayipempherera mipangoyo; ndiyeno pali inanso pano usikuuno. Kotero, ife—ife tikukhulupirira kuti Mulungu amachiza odwala. Maumboni ochuluka kwambiri a machiritso pakati pathu, ndi mdziko lonse, ndipo ndife oyamikira pa ichi.

⁷ Ndipo ine ndinaganiza, Lamlungu lotsatira, pokhala ine ndiyenera kuti ndikhale nditachoka kwa pang'ono pokha, ndipo ife takhala tiri kuchititsa yochuluka kwambiri ya kuphunzitsa chabe ndi ya Uthenga, potero ine ndinaganiza icho chikanakhoza kukhala chinthu chabwino ngati ife tikanakhala nawo—msonkhano wamachiritso, kupempherera odwala. Ndipo ife tikudalira kuti Mulungu adzatipatsa ife nthawi yaikulu.

⁸ Tsopano, ambiri a inu muchita kuwongolera mailosi ambiri usikuuno. Kotero ine ndinali kuyankhula kwa magulu uko ku—Blue Boar Cafeteria, lero, kumene ine ndinali kulandira chakudya. Anthu ambiri abwino, ine ndiyenera kuti ndigwedeze manja awo ndi kuyankhula ndi iwo, anthu amene ine sindinakumanepo nawo kale, amene amabwera kuno ku tchalitchi. Ndipo ine ndiri woyamikira chifukwa cha abwenzi oterowo, ndipo ine ndikufuna ndithokoze mmodzi ndi wina aliyense wa inu. Ena a iwo anatchera nthuza zakuda, ndipo atibweretsera ife. Ndipo amodzi anatibweretsera ife chibekete cha manyuchi, kapena uchi, ine ndikukhulupirira iwo unali, ndi—ndi zinthu basi. Inu simukudziwa chimene icho chikutanthauza. Ndipo kwa mmawa, ine ndimabwera ndi kutuluka mu nyumba, nthawiyina uko . . .

⁹ Mmawa wina uko analipo m'bale wina kumeneko amene anali moyipa kwenikweni, analibe zovala ndi zinthu, amafuna kuti ine ndipite ndikamupezere iye zovala zina. Ine ndinayamba kumapita, ndipo ine pafupifupi ndikanapunthwira pa chibekete cha nthudza zakuda chiri pamenepo. Ine ndinati, “Kodi inu munabweretsa nthudza zakuda izi?”

¹⁰ Ndipo iye anati, “Ayi, palibe kalikonse kamene ndinachita ndi icho. Ine ndakhala ndiri pano kuwala kwa tsiku kusanayambe, ndipo izo zinali ziri apa pamenepo.” Ndipo uyo anali M'bale wanga wabwino Ruddell amene anawabweretsa iwo kwa ine. Ndipo, chotero, zinthu zimenezo ine ndithudi ndikuziyamikira.

¹¹ Billy Paul wangofotokoza kumene kwa ine, mphindi zingapo zapitazo, kuti pakati pa osonkhana awa usikuuno, iwo anali atatenga chopereka, kuti cha ine. Ine—ine ndikukuthokozani inu pa izo. Ine sindinafuno inu kuti muchite zimenezo. Ine—ine ndikungoyamikira kuyesetsa kwanu, ndi zina zotero, koma izo

sizinali zofunikira. Ndipo, koma, Ambuye akudalitseni inu. Inu mukudziwa, inu mukudziwa, Baibulo linati, “Mwa kuchuluka monga inu mwachitira kwa aang’ono a awa, inu mwachitira izo kwa Ine.”

¹² Tsopano, ine ndakhala ndiri ngati ndimalankhula kwa inu, pa Uthenga, molunjika kwambiri. Ndipo ine... Anthu ena akhoza kukhala pansu pa kulingalira kuti—kuti ine ndikuganiza kuti Yesu abwera mmawa kapena usikuuno. Ine ndikutero. Tsopano, ine sindikunena kuti Iye atero. Ndipo, panonso, Iye mwina sangabwere kwa sabata ikudzayo, ndipo icho chikhoza kukhala chaka chotsatira, izo zikhoza kukhala zaka khumi. Ine sindikudziwa liti Iye ati adze. Koma, pali chinthu chimodzi ine ndikufuna kuti... nthawizonse inu musunge mu malingaliro, inu mukhale okonzeka miniti iliyonse kapena ora. Mwaona? Kuti, ngati Iye sabwera lero, Iye akhoza kukhala pano mawa. Kotero ingosungani icho mu lingaliro lanu, kuti Iye ali kubwera.

¹³ Ndipo ine sindikudziwa nthawi yanji yomwe iti ikhale ora langa lotsiriza pa dziko lapansi ili, palibenso wina wa ife akudziwa. Ndipo palibe mmodzi wa ife akudziwa liti limene iye ali kudza. Iye sakudziwa, ngakhale Mwiniwake, mwa Mawu Ake Omwe; Iye anati, “Atate, okha, akudziwa liti Iwo ati adzabwere; osati ngakhale Mwana akudziwa liti Iye ati adzabwere.” Ndi pamene Mulungu amutumiza Iye kwa ife kachiwiri. Koma ife tiri kuyang’anira Kudza Kwake. Ndipo ngati Iye sabwera mu m’badwo wanga, Iye akhoza kubwera mu wotsatira; ngati Iye sati abwere mu umenewo, Iye adzabwera mu wotsatira. Koma, kwa inendekha, ine sindikukhoza kuwona nkome nthawi iliyonse yomwe yatsalira. Ine basi... Kwa ine, izo zikanakhoza kuchitika pa miniti iliyonse. Tsopano, izo siziri kutanthauza... Izo siziri kutanthauza, tsopano, kuti inu mudzaona miyamba ikusintha ndipo chirichonse... Uko sindiko Kudza kumene ine ndikukunena. Ine ndikunena za Mkwatulo.

¹⁴ Mwaona, Iye akupanga Kudza kutatu. Iye akudza mu Maina atatu, a Ana. Iye anabwera mu utatu; Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Onani, zonse izo Khristu yemweyo, Mulungu yemweyo, nthawi zonse. Tsopano, ife tikudziwa Iye akubwera kuti abweretse ntchito zitatu za chisomo; kulungamitsidwa, kuyeretsewa, ubatizo wa Mzimu Woyera. Chirichonse, mwa Mulungu, chimatsirizidwa mu mautatu.

¹⁵ Ndipo kotero Iye anadza, poyamba, kuti adzawombole Mkwatibwi Wake. Iye akubwera, kachiwiri, monga Mkwatulo, kudzamutengapo Mkwatibwi Wake. Iye akubwera, kachitatu, ndi Mkwatibwi Wake, Mfumu ndi Mfumukazi; zitachitika, ndi pamene anthu ambiri akuyembekezera Kudza.

Koma pamene Iye akubwera nthawi iyi, osati aliyense koma iwo amene ali okonzeka adzadziwa pamene Iye akubwera. Apo padzakhala kusowa chabe kwa anthu. Iwo sadzadziwa chimene

chinachitika kwa iwo. Iwo adzangokhala atatengedwa napita, mu kamphindi, ndipo kuti iwo azidzangopezeka atasowa. “Atasinthidwa mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso.” Kotero ingokhalani okonzekera izo. Icho chidzakhala chowopsya mmawa wina kuti umusowe wokonedwa mmodzi, palibe mmodzi angakhoze kuwapeza iwo. Kodi icho sichikanakhala choyipa kwambiri kuti udzadziwe kuti iwo wachitika kale ndipo inu mwawuphonya iwo? Kotero ingokhalani pamaso pa Mulungu.

¹⁶ Tsopano, sabata lotsatira, Ambuye akalola, Lolemba lotsatira, kuchokera sabata la kuchokera Lolemba ili, ngati Mulungu alola, ine ndikutenga banja lanja kubwerera kupita ku Arizona kumene iwo amapita ku sukulu, ndiye ine—ine ndikabwerera.

¹⁷ Tsopano, ine sindimapita kunja uko...Ine ndiribe misonkhano iliyonse yoti ndikhale ndiriko kumeneko. Ine sindikhala ndiri mu Arizona mokwanira. Ine ndimapita kwina kwake. Ine ndimutengera mkazi wanga kupita kumeneko, Lolemba lotsatira. Ine ndikubwerera kuno kachiwiri. Ine ndidzachokera kuno kupita ku British Columbia. Ine ndidzabwerera kachiwiri ku Colorado. Ine ndidzakhala ndiri mu Arizona kachiwiri nthawiyina poyandikira Khristimasi, kwa maminiti pang’ono chabe, utali wokwanira...mwinamwake masiku awiri kapena atatu, kulitengera banja palimodzi, kukhala titabwerera kuno kupyola matchuthi a Khristimasi, Ambuye akalola, kukhala ndi msonkhano mpaka mu sabata la chaka chatsopano pano.

¹⁸ Kotero ndiye ine ndiri kuno, mwakuchitika, mochuluka. Ine ndiri kuno kakhumi kuposa kunja uko, chifukwa ife tiribe mpingo uliwise kapena misonkhano iliyonse kunja uko, palibe chimene ife tiri nacho kunja uko, chotero, kwa njira ya msonkhano wa mpingo. Ndicho chinthu chimodzi choyipa cha uko. Ine ndiribe malo oti ndiziwatumizako ana kumene iwo akanati azikamva Uthenga uwu, monga momwe ana anu amakhala akumvetsera iwo kuno, ndipo—ndipo kotero ndicho cholakwika chimodzi chomwe ife tiri nacho. Koma iwo onse ali athanziko. Ndi kowuma, kotantha, nyengo youma, koma ana onse akuwoneka kuti ali athanziko. Ine sindikhala kumeneko motalika kokwanira kuti ndidziwe ngati ndi kwa thanziko kapena si kwa thanzi, Ine, ine ndimakhala ndiri koyenda ndipo ine—ine—ine ndikuganiza ine ndinangobadwa woyendayenda.

¹⁹ Mkazi wanga amanditcha ine...ine ndikudziwa kuti iye ali pano, kotero ine ndipezana nazo izi tikatuluka tchalitchi, inu nonse mukudziwa. Kodi chimatchedwa chiyani chija, mphepo yosuntha, kapena mphepo yosapumira, kapena chirichonse—chirichonse, inu mukudziwa, mchenga wosuntha? Kapena, ine nthawizonse ndimakhala ndiri paulendo, mwakuyankhula kwina. Ndipo ine ndakhala wokwatira tsopano, zaka makumi

awiri ndi ziwiri, ndipo ine nthawizina ine ndimaganiza ndine mlendo pa nyumbayo, chifukwa ine ndimayenera kuti ndizipita.

Koma ine ndikuyembekezera nthawi yomwe ife titi tidzakhazikike mu Dziko la kwathu tsiku lina. Koma tsopano nk'hondo ili kupitirira, kotero tiyeni tikhale mu pemphero.

²⁰ Musati muyiwale, Lamlungu lotsatira mmawa, Ambuye akalola, mudzabweretse mkati odwala anu ndi osautsika. Bwerani molawirira, tengani malo anu, ndipo mwinamwake pali gulu loti lidzapemphereredwe. Ife tidzayenera kupereka makadi a pemphero. Ngati palibe okwanira, ife sitidzapereka makadi a pemphero, okwanira okha kuti tidzapange mzere wawung'ono wonga madazeni awiri kapena atatu, kapena chinachake. Koma ife—ife mwinamwake tidzapereka makadi a pemphero, kotero ife mwinamwake tidzachita izo pafupi ora usanayambe msonkhano wanthawizonse, umene ine ndikuganiza ukuyambika... Iyo idzakhala eyiti, eyiti kapena hafu pasiti eyiti, iwo azidzapereka makadi a pemphero; kutsegula tchalitchi, kupereka makadi a pemphero Lamlungu lotsatira mmawa. Ndiyeno mukhale otsimikiza kuti mudzakhale kuno chifukwa cha anu... Mudzabweretse okondeka anu, dzawayikeni iwo mkati mmenemo. Mudzakhala mwabwino ndi mozizira mu tchalitchi, ngati iwo akudwala, ndipo ife tidzachita chirichonse chimene ife tingakhoze kuti tiwapempherere iwo.

²¹ Ndikukuthokozani inu, kachiwiri, chifukwa cha chopereka chachikondi.

²² Ndipo tsopano ife tiwerenga ena a Mawu a Mulungu, usikuuno, ndi kukhala okonzekera chochitika ichi cha Kukhalapo Kwake panonso kuti atibweretsere ife Mawu Ake. Tsopano, ife tikudziwa kuti ife tikhoza kuwerenga ndime, koma Mulungu ayenera kuwulula nk'hani yake. Mwaona? Ife tikhoza kutenga ndime, koma Mulungu ayenera kuwulula nk'hani yake. Ndipo pamene inu mukutembenuza tsopano mu Bukhu la Yereimiya, mutu wa 2.

²³ Ine ndikufuna kunena kuti ndine wokondwera kukhala, ali nafe, M'bale Lee Vayle, m'bale wofunika mwa Ambuye. Ndipo ine ndikuganiza pano, m'bale pano, ine sindingakhoze kuganiza za dzina lake, M'bale Willard Crase. Ndipo ine ndawawona abale ochokera ku Arkansas, M'bale John ndi iwo, ochokera kozungulira Poplar Bluff, ndi M'bale Blair. Ndi, o, M'bale Jackson, ndi M'bale Ruddell, ndi ochuluka chotero amene ine—ine sindingakhoze basi... Ndikukhumba ine ndikanakhoza kutchula dzina la aliyense, koma ine sindingakhoze basi kuchita izo, ndipo inu mukumvetsa. M'bale Ben Bryant, ine ndikumuwona iye wakhala kuno; iye ali nthawizonse ngodya yanga ya ameni pamene ine ndiri... Aliyense akumudziwa Ben mwa liwu lake. U-nhu.

²⁴ Ife, titakhala mu California nthawi yina, ine ndinali kulalikira Uthenga kwa anthu Achibaptisti uko mu chigwa. Iwo anali ndi hema wamkulu kumeneko, ndi ochuluka okhala ngati Achibaptisti apamwamba. Ine sindimakhoza konse kumumva “ameni” kuchokera paliponse; inu mukudziwa, kuchita mantha kuti ena a akazi angafute utoto pa nkhope zawo. Ndiyeno, chinthu choyamba inu mukudziwa, ine ndinawona mapazi awiri pafupi monga *chonchi*, akupita mmmwamba mu mlengalenga, ndi manja awiri aakulu, ndi tsitsi lakuda likugwadera pamenepo, akufuula, “Ameni,” akukuwa monga choncho. Ndipo ine ndinayang’ana pansi, ine ndinati, “Ben, iwe wachokera kuti?” Iye analidi kupeza “ameni.”

²⁵ Ine ndinamuwona mkazi wake akumuyang’anitsitsa iye, pang’ono pokha. Chabwino, iye akutaya pang’ono la tsitsi lakuda ilo, koma ndizo zonse zabwino, inu mukudziwa. Musati mudandaule ndi izo. Ine ndinatero, langa, nthawi yaitali kale.

Kotero, tsopano, musati muyiwale kumapemphera.

²⁶ Tsopano pamene ife tikufika ku mbali yodzipereka ya msonkhano, kumbukirani, ngati ife tiwerenga Mawu awa, ndiye Mulungu awadalitsa Mawu Akewo. “Iwo sadzabwerera kwa Iye mwachabe, koma Iwo adzakwaniritsa icho chomwe Iwo analingaliridwira.” Ndipo ine ndikudziwa, mu kuwerenga Mawu, ine ndidzakhala nthawizonse ndiri kulondola. Pamene ine ndiwerenga Mawu, Mulungu adzawalemekeza Mawu Ake.

²⁷ Tsopano tiyeni ife tiyime mwa kulemekeza ku Mawu Ake. Yeremiya, mutu wa 2, ndime za 12 ndi 13 za Yeremiya 2.

Khalani ozizwitsidwa, O...miyamba, pa ichi, ndipo khalani owopa kwambiri, khalani inu abwinja kwambiri, atero Yehova.

Pakuti anthu anga achita zoyipa ziwiri; iwo anandisiya ine kasupe wa madzi amoyo, ndipo iwo adzibowolera zitsime, zitsime zong’aluka, zomwe sizingakhoze...sizingakhoze kusunga madzi.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano.

²⁸ Wokonedwa Mulungu, Mawu Anu awerengedwa kale. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu muwalemekeze Mawu amenewo ndi kupereka kwa ife usikuuno fanizo kapena choyendera limodzi ndi Iwo; pamene ife tikuyang’ana ku masiku amene apita, Israeli, monga zitsanzo, monga Baibulo limatiphunzitsira ife kuti ife tikhoza kuwona chimene Inu munachita kwa iwo pamene iwo anawamvera Mawu, kuwona chomwe Inu munachita kwa Iwo pamene iwo sanawamvere Mawu, ndi kuphunzira chomwe ife tiyenera kuchita. Kotero, ife tikupemphera kuti Inu muyankhula kwa ife usikuuno mwa njira yapadera kwambiri, kuti ife tikhoze kudziwa momwe tingadzichititsire tokha mu tsiku lino, lomwe ife tinaphunzira

mmawa uno umene ife tiri kukhalamo. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

Mukhoza kukhala.

²⁹ Ine ndikufuna kuyankhula usikuuno pa phunziro, kwa basi—nthawi yayifupi pa: *Zitsime Zong'aluka*.

³⁰ Israeli anali atachita zoyipa zazikulu ziwiri. Mulungu anati iwo anali atatembenuka kuchoka kwa Iye, Kasupe wa Moyo, ndipo anali atadzibowolera iwo okha zitsime zoti azimwa kuchokeramo. Tsopano, ndicho chinachake.

³¹ Chifukwa chimene ine ndinaganiza za ndime iyi chinali chifukwa chakuti iyo ikanayenda limodzi ndi chimene ine ndinali kuyankhula mmawa uno, za ora limene ife tikukhalamo, ndi Chifukwa chimene ife tiri kuchikangamira.

³² Ndipo ife tikuyang'ana pa Israeli monga chitsanzo, kuti, chimene Mulungu anali, Iye nthawizonse ayenera kukhalabe chomwecho. Ndipo pali chinthu chimodzi chokha chimene Mulungu anayamba walemekezapo, chimenecho chinali, njira Yake imene Iye anayipereka kwa anthu. Ndipo pamene iwo anatuluka mu njira imeneyo, ndiye Mulungu anali wosalemekezedwa, ndipo Mulungu anawapanga anthuwo kuzunzika chifukwa chochoka ku chimene Iye anali atawauza iwo kuti azichichita, zinalibe kanthu chomwe icho chinali.

Iye ngakhale anawapatsa iwo lamulo, “Musati mukhudze, musati mugwire, musati mulawe.” Osati chabe chifukwa cha kuyipa kwa kuchita icho, koma kuyipa kwa kusamvera chimene Iye anati zichitani. Ndipo pali nthawizonse kuti sipangakhoze kukhala lamulo popanda chilango cha lamulo. Chifukwa, ngati palibe chilango, ndiye lamulo siliri lochuluka kwa ilo kupatula ngati ilo liri ndi chilango. Lamulo!

³³ Tsopano, ife tikupeza, zimene iwo anachita mu tsiku limenelo zikuwoneka zoyendera limodzi ndi zimene ife tikuchita lero, zimene anthu a mpingo akuchita.

³⁴ Tsopano ife tikuwona chinthu chachirendo apa. Icho mwina chikhoza kukhala chachirendo kwa anthu ena, pamene Iye anati, “Inu mwatero, iwo atero, adzibowolera kwa iwoeni zitsime, zitsime zong'aluka.” Tsopano, mwinamwake ena a inu simukudziwa chomwe chitsime chiri. Ndi angati akudziwa chomwe chitsime chiri? Chabwino, pafupi nonse a inu. Ngati inu munayamba mwaleredwerapo pa faramu, inu mukudziwa chomwe chitsime chiri. Ine ndikukumbukira ine ndinamwapo zipumbu zokwanira kuchokera mu chimodzi, kuti—kuti ndidziwe chomwe chi—chitsime chinali.

Ndinkalalikira kunja kumudzi kumene, mu tchire lamdima, kumene iwe umakhala ndi chikho chachikulu chodzaza ndi madzi apa chitsime chiri pamenepo, kuchokera mu—mvula, inu mukudziwa, ndipo icho chimakhala ngati chokalambirapo

pang'ono. Ndipo—ndiyeno zipumbu, pa nthawi yausiku, zimalowa mu icho. Ndipo koteru ine ndikudziwa chomwe madzi a pa chitsime ali.

³⁵ Chi—chitsime chiri m—malo, chinthu chomwe chimakumbidwa mu nthaka, kuti chitenge malo a kasupe. Kumene anthu alibe mpope, ndiye iwo amatenga—chitsime. Mwa kuyankhula kwina, chitsime ndi thanki lopangidwa ndi anthu kapena chitsime chopangidwa ndi anthu mu nthaka, chimene anthu amachikumba, kuti azitungapo madzi, kuti—kuti aziwagwiritsa ntchito iwo. Ena a iwo amachigwiritsa ntchito icho kukhala madzi achapira, ndipo ena amachigwiritsa ntchito icho kukhala madzi akumwa, ndi njira zosiyana, mwinamwake. Madzi onse nthawizina, amene ife tinali kuwatunga, anali a pa chitsime. Ife tinali ndi kanthu kakang'ono kamene iwe unkachita kumakapukusa, mozunguliza, kuzunguza, kuzunguliza, kuzunguliza, kuti madziwo atuluke; tinali ndi zibete zazing'ono pa icho, kuti tizipopera madzi kuchokera mu chitsimecho.

³⁶ Chabwino, ife tikuzindikira chinthu chimodzi chokhudza chitsime chimene chiri chosiyana ndi mpope. Tsopano, chitsime chimafika pouma. Chi—chi—chitsime sichingakhoze kudzidzazitsa chokha. Icho ndi—ndi... Si chiri chodalirika. Iwe sungakhoze kudalira pa chitsime. Icho chiyenera kudalira ndi kuyembekezera pa mvula yomwe imavumba mu chirimwe kapena mu dzinja, chirichonse chimene chiri... Kawirikawiri, mu nthawi ya dzinja pamene chisanu ndi mvula zimabwera, ndiye izo zimayendetsa madzi kupita mpaka mu chitsime. Ndipo ngati icho sichitenga madzi amenewo, ndiye inu—inu simumakhala ndi madzi aliwonse. Icho chonse—icho chonse... chimauma. Ndipo icho sichingakhoze kudzidzazitsa ichochokha. Chitsime chachikalecho sichingakhoze kudzidzazitsa chokha. Icho chimalandira kudzazitsa kwake kuchokera ku—mvula imene imavumba.

³⁷ Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzindikire chinthu china chokhudza chitsime. Kawirikawiri, inu mudzapeza, kapena momwe izo zinaliri ku malo athu, chitsime... Kawirikawiri barani limakhala pafupi kawiri muyezo wa nyumba, ndipo iwo kawirikawiri amawayendetsa madzi kuchokera ku barani, kupita ku chitsime. Ine ndikukumbukira chitsime chimenecho kunjika kumene uko, pamene iye anali... pamene ma—mapaipe odzeretseramo ankawapititsa iwo mkati, aponso, kuchokera ku barani. Icho chinkadzaza ndi ochokera pa barani.

Koteru ndiye madzi amatengedwa kuchokera pa denga la barani; kumene, nyama zonse zimapondapapo pozungulira kudzera ku bwalo la khola, ndi nyansi zonse za kuseri kwa barani zimakadikha pamwamba pa barani, mu nthawi yowuma. Ndiyeno madziwo amabwera ndi kusesera izo zonse pansu kuchokera pa dengalo, kupita mu dzenje lopangidwa

ndi munthu, ndiye kupita mu chotsanulira chopangidwa ndi munthu, kenako nkupita mu chitsime chopangidwa ndi munthu. Ndipo ngati inu si muli ndi nyansi, ine sindikudziwa chimene inu muli nacho, pamene inu muli ndi chitsime. Inde, bwana! Ndi zonse zopangidwa ndi munthu, ndi chauve basi monga icho chingakhoze kukhalira.

³⁸ Inu mukudziwa, ife tinali kuchitcha...Ife tinali ndi chiguduli chosefera pa chimodzi. Kodi inu munayamba mwadziwapo chomwe icho chinali? Tinkachita kuyika sefa ya chiguduli pa icho, kuti chidzigwira zipumbu zonse ndi zinthu zimene zimabwera kuchokera pamwamba pa—barani, ndi pa malo ponse pozungulirapo, ndi kutsanulikira pansu kuchokera pa malo amodzi kupita ku amzake, kupita mu chitsime. Ndipo ife tinali kumayikapo—sefa ya chiguduli pa icho, kuti chidzigwira zonse—zauve ndi zinthu zimene ife tikanakhoza. Zooni, icho sichikanakhoza kugwira nyansi zenizeni, icho chinkangogwira zibuluma zazikulu zimene zinkabwera pansu ndi kugwera mu icho. Chipumbu chikhoza kugwera mu icho, koma maliroliro a chipumbucho ankapitirira ndi madziwo. Kotero, inu—inu munkakhala kwenikwenidi ndi nyansi pamene inu mukhala ndi chitsime chapadothi.

³⁹ Mu masiku pang'ono, inu mukawasiya madzi amenewo kuti akhale mmenemo, ndipo iwo amakhala chithaphwi. Inu mukawasiya madzi kuti akhale mu chitsime, iwo amakhala chithaphwi. Ndipo icho chinakhala chodzaza ndi—ndi achule, ndi abuluzi, ndi njoka. Ndipo ife tinali kuzitcha izo “mbululu,” tating'ono kwambiri. . . Ine sindikudziwa ngati. . . Izo sindizo nthata, izo ndi. . . ine sindingakhoze, ine sindikudziwa chomwe inu mumazitcha izo. Koma kanthu kena kakang'ono kamalowa mu madzi, kamene—kamene ife tinkakatcha iko mbululu. Inu mukudziwa chomwe izo ziri. Ndi angati amene akudziwa chomwe ine ndikuchikamba? O, bwanji, zedi, nonse inu anthu a kumidzi mukudziwa. Izo zimawapangitsa iwo onse kudzaza ndi zithaphwi, ndiyeno okonda zithaphwi awa amabwera ndi iwo. Izo zimangobwera kumene, chifukwa iwo anachita chithaphwi. Ndipo chifukwa kuti iwo achita chithaphwi, iwo amakopa tizinyama pamenepo tomwe timakonda zinthu zachithaphwi.

⁴⁰ Ndipo ndicho chinthu chonse chonga mipingo yathu lero. Ine ndikuganiza kuti ife tasiya. . . Limodzi la machimo aakulu amene mpingo wachita lero, kungokhala monga Israeli pamenepo, iwo anamusiya Iye, Kasupe wa Madzi amoyo, ndipo adzibowolera okha zitsime zopangidwa ndi anthu. Ndipo mwakhala mokhalamo mwa chirichonse chimene chimakonda madzi a mtundu umenewo. Abuluzi, achule, ndi mitundu yonse ya majeremusi osayera, zimakhala mwa icho, chifukwa ndi thanki lopangidwa ndi munthu. Ndipo mu thanki ili zinthu izi zimakhalamo, chitsanzo changwiwo cha zipembedzo zathu lero.

41 “Tsopano,” inu mukuti, “M’bale Branham, nchifukwa chiyani inu mumamenya pa anthu amenewo molimba kwambiri?”

Iwo ayenera kuti azimenyedwapo. Iwo ayenera kuti azimenyedwapo. Thawani izo, chifukwa izo potsiriza zidzapanga chilemba cha chirombo. Kumbukirani, icho ndi Choonadi! Icho chidzakhala chilemba cha chirombo. Chipembedzo chidzatsogolera kumene ku icho. Icho chiri pa ulendo wake wopita kumeneko tsopano, kuti chikakamize, mwa mphamvu.

42 Yang’anani mu ufumu wakale wa Chiroma. Ndicho chimodzimidzi chimene chinawatsogolera iwo ku chilemba cha chinyengo chimenecho. Inu munapeza kuti panalibe munthu yemwe akanakhoza kugula kapena kugulitsa wopanda chilemba cha chirombo. Iye amayenera kukhala nacho icho.

43 Pali makalasi awiri okha a anthu ati adzakhale pa dziko lapansi; awo okhala ndi Chisindikizo cha Mulungu, ndi iwo okhala ndi chilemba cha chirombo. Makalasi awiri okha, kotero iwe udzayenera kudzakhala ndi chimodzi kapena chimzake. Icho chidzakhala chinyengo, chi—chilemba cha—cha chipembedzo, chipembedzo chachinyengo.

44 Ndipo icho chidzakhala ndi fano kwa chirombo. Pamene ife tikuwerenga, ife tikuzipeza kuti Roma anali, ali, ndipo nthawizonse adzakhala ali, chile-...kapena, chirombo. Chimodzimidzi. Palibe njira yotengera icho mwa china chirichonse. Roma!

45 Ndipo kodi Roma anachita chiyani? Anatembenuzidwa kuchokera ku Roma wachikunja kulowa mu Roma waupapa, ndipo anapanga bungwe kachitidweko, kachitidwe ka ponseponse, kamene kanakakamiza aliyense kupita mu chipembedzo chimodzi icho kapena kuyikidwa ku imfa.

46 Ndipo ndi chinthu chachirendo kuti United States uyu akuwoneka powonekera, ndipo ali monga mwanawankhosa. Ndipo mwanawankhosayo ali ndi nyanga ziwiri zazing’ono, maufulu aboma ndi azauzimu. Ndipo patapita kanthawi, pamene uyo anali mwanawankhosa, ife tikupeza kuti iye anayankhula ndiye monga chinjoka ndipo anachita ndi mphamvu zonse zomwe chinjoka chinali nazo asanafike iye. Ndipo Baibulo likuti uza ife kuti iwo ananena kuti, “Tiyeni ife tipange fano kwa chirombo.” Fano ndi chinachake chonga chinthu chinachakenso. Ndipo ife tikhoza kuwona icho pakali pano kuti, mu chikhalidwe chake chachinyengo, mpingo ukupanga Mgwirizano wa Mipingo ya M’dziko, lomwe liri fano ku mphamvu ya Roma; ndipo adzakakamiza pa anthu chinthu chomwecho chimene Roma wachikunja anachita... kapena Roma waupapa anachita. Kotero, palibe njira yina, palibe chinthu china. Koma icho ndi Choonadi.

47 Ndipo ndicho chifukwa ine ndikuzimenya izo mu m'badwo wanga, mu nthawi yanga, chifukwa icho chiyenera kuti chizimenyedwa. Kuyitana kunabwera mkati, konena, "Tulukani mwa iye, anthu Anga, kuti inu musakhale ogawana naye za machimo ake!"

48 Tsopano, ine ndikufanizitsira izo ku zonyansa izi, zitsime zauve. "Iye ndiye Kasupe wa Moyo. Iye ndiye Madzi amoyo." Ndipo munthu akumusiya Ameneyo, ndi kudzikumbira okha zitsime zomwe zingakhoze kokha kugwira nyansi. Ndicho chinthu chokha chomwe izo zingakhoze kugwira. Ndipo ndicho chimene zachipembedzo zimachita; izo zimagwira chirichonse chomwe chimabwera motsatira ndi kufuna kujowina. Iwo ali lolera kuzitenga izo ngati ziri ndi ndalama zina kapena zikhoza kumavala mwa njira inayake. Ziribe kanthu kuti iwo ndi ndani, kumene iwo amachokerako, iwo amawatenga iwo, mulimonse.

49 Tsopano ife tikupeza, apanso, kuti, chilemba cha chirombo ichi chimene chinapangidwa apa. Amerika, ali, chiwerengero cha khumi ndi zitatu. Iye anabadwa ndi zigawo khumi ndi zitatu. Iye anali ndi mbendera imene inali ndi nyenyezi khumi ndi zitatu, milozo khumi ndi itatu. Ndipo iye akuwonekeranso mu Chivumbulutso mutu wa 13. Ndipo Amerika nthawizonse wakhala ali mkazi, akuyimiridwa pa ndalama zathu. Ngakhale mutu wa Chimwenye, pa kobidi, pali nkhope ya mkazi. Ife tikudziwa zimenezo, tikudziwa mbiriyakale ya izo. Chirichonse, Belu la Ufulu, ndi china chirichonse, ufulu. . . Fano la Ufulu liri, chirichonse, mkazi. Mkazi, chiwerengero cha khumi ndi zitatu. Mwaona? Tsopano, ndi—ndi chokongola kuti uwone zinthu zimenezo.

50 Ndipo tsopano ine ndaneneratu mwa vumbulutso lochokera kwa Mulungu, kapena masomphenya mu 1933, kuti zinthu zisanu ndi ziwiri zikanachitika isanafike nthawi yotsiriza. Ndipo kuti, chimodzi cha izo, kuti, "Mussolini," yemwe anali pamenepo akukhala wolamulira mwankhanza, "iye akanakhala wolamulira mwankhanza. Ndipo, aponso, iye akanadzapanga kuwukira ndi kupita uko ku Ethiopia, ndipo akanakatenga Ethiopia. Ndipo Mzimu, Iwo unati, 'Iye adzagwa pa mayendedwe ake.'"

51 Ine ndikudabwa ngati alipo aliyense wa a nthawi-yakale amene watsalirabe mu kachisi, amene akukumbukira ine ndikunena zimenezo mu Holo ya a Redman kumusi kuno pamene ife tinkalalikira, zambiri, zaka zambiri zapitazo. Kodi alipo mmodzi mu chipinda chino, usikuuno, yemwe watsalira kuchokera kumusi uko ku Holo yakale ya a Redman pamene ine ndinalalikira zimenezo, pamene iwo anali atatulutsa N.R.A., kale mmbuyo mu nthawi ya Roosevelt kulamulira koyamba? Ine ndikuganiza mulibemo mmodzi mkati muno. Kodi alipo mmodzi? Eya, eya, mmodzi, alipo mmodzi. Inde, Akazi a Wilson, ine ndikuwakumbukira iwo. Mkazi wanga, wakhala

kumbuyoko. Awiri atsalira, kuchokera mwa m’badwo wakale wa iwo mu tsiku limenelo.

Kuti, pamene iwo ananena kuti N.R.A. iyi inali chilemba cha chirombo, ine sindinanene, “Kalikonse kwa izo; osati nkomwe. Chilemba cha chirombo sichingachokere kuno. Icho chichokera ku Roma. Ndipo icho sichingakhoze kukhala chilemba cha chirombo.”

⁵² Ndipo tsopano kumbukirani kuti zinthu izi zinanenedwa. Ndinati, “Adolph Hitler akanafika ku mathero achinsinsi. Ndipo iye akanalengeza nkondo pa United States. Ndipo iwo akanamanga chachikulu—chi—chinthu chachikulu cha konkire, chimene iwo akanati ngakhale azikhala mu icho. Ndipo apo pomwe Amerika akanalandirapo kumenyedwa kowopya, pa ichi.” Ndipo iwo unali mzere wa Siegfried, zaka khumi ndi chimodzi iwo usanayambike kumangidwa nkomwe. Ndiyeno anati, “Koma iye akanafika ku mathero; ndipo States akanadzapambana nkondoyo.”

⁵³ Ndiyeno ananena, kuti, “Pakhala pali ma ism atatu; Nazism, fascism, ndi communism.” Ndipo ine ndinati, “Izo zonse zidzathera mu communism. Russia akanadzatenga izo zonse, mu chikominsi.”

⁵⁴ Ndipo ine ndinati, “Ndiye sayansi idzafika podzakhala yaikulu kwambiri, munthu adzafika pokhala wanzeru kwambiri, mpaka iye adzayambitsa zinthu zambiri chotero mpaka kuti iye adzapanga galimoto yomawoneka monga dzira, yomwe iti idzakhale chokhala ngati denga la galasi pa iyo, ndipo iyo ikanati izidzayendetsedwa ndi mphamvu inayake osati chiwongolero.” Ndipo iwo ali nayo galimotoyo.

⁵⁵ Ndipo ine ndinati, “Ndiye makhalidwe a akazi athu adzafika pakugwa mu zinthu zotsika chotero, mpaka iwo adzakhala chamanyazi kwa mafuko onse. Iwo azidzavala zovala zachimuna. Iwo adzakhala akupitirira kumavula zovala zawo mpaka iwo azidzabwera pansu kumene ngati kuti angovala zovala zamkati zawo, zokhazo basi. Ndipo, potsiriza, iwo adzafika pomavala tsamba la mkhuyu chabe.”

Ndipo ngati inu mutazindikira, mu *Life* magazini ya mwezi watha, iwo anali ndi mkazi atavala masamba a mkhuyu. Ndipo ndiwo mkanjo watsopano wausiku, kapena mwinjiro, zomwe iwo amavala usiku; zamberewere, ukhoza kupenya kupyola mu izo, masamba a mkhuyu okha akungobisa malo ena okha a thupi lake, zopanda zingwe, kapena chingwe, zovala zosambira zopanda zomangira, pamwamba pa izo, thupi lapoyera. Ndipo momwe kuti zinthu zimenezo zachitika!

⁵⁶ Ndiye ine ndinati, “Ine ndinamuwona mkazi ataima mu United States, monga mfumukazi yaikulu kapena chinachake. Ndipo iye anali wokongola kumuyang’ana pa iye, koma woipa

mu mtima wake. Ndipo iye anapangitsa mayendwe a fuko, kupita mwa mayendedwe ake.”

⁵⁷ Ndiye ine ndinati, “Potsiriza, Iye anandiuza ine kuti ndiyang’ane mmbuyo Kummawa kachiwiri. Ndipo, pamene ine ndinatero, ine ndinawona, zinkawoneka monga, momwe izo zinaliri, dziko linali litaphulika. Ndipo kutali komwe ine ndikanakhoza kukuwona, panalibe kanthu koma timitengo, ndi—ndi miyala yamoto inali itaphulitsidwa kuchokera pa dziko lapansi.”

Ndipo izi zinali zoti zichitike asanafike mapeto a dziko. Ndipo zisanu za zisanu ndi ziwiri zachitika kale, mu zaka makumi atatu ndi zitatu. Apo ife tiri, kubwerera ku nthawi yotsiriza!

⁵⁸ Ndipo ine ndinayankhula motsutsa kachitidwe ka zipembedzo ako apo pomwe. Ndipo ine ndikanali kukhulupirira, usikuuno, kuti ndi dziwe lauve, kuti ndi malo kumene nyansi zimathamangira kulowa mu ilo. Ine sindingakhoze kukhulupirira kuti Mulungu angakhoze kuchitengera chinthu choterocho mu Mpingo Wake, chifukwa icho chiyenera kuti chibadwe mwa Mzimu wa Mulungu ndiyeno nkuyeretsedwa icho chisanafike poti chitchedwe Chake. Thupi lachinsinsi la Khristu, ife timabatizidwa kulowa mu Ilo mwa ubatizo wa Mzimu Woyera.

⁵⁹ Inde, kachitidwe ka chitsime aka kali ndithudi chitsanzo changwiwo cha chipembedzo. Munthu wanzeru ayenera kuyang’ana, ndipo nkusapita konse mu izo, pakuti Mulungu watimikizira kupyolera mu mibadwo kuti Iye akutsutsana nazo izo ndipo sanagwirepo konse ntchito ndi izo. Gulu lirilonse . . . Nthawi iliyonse munthu akawuka ndi uthenga, monga Lutera, Wesile, kapena ena otero, ndi Smith, ndi Kalvini, ndi iwo; pamene iwo anayambitsa bungwe, Mulungu anayika chinthucho pa alumali ndipo sanati adzachichezere konse icho kachiwiri mu chitsitsimutso.

⁶⁰ Penyani kupyola mu mbiriyakale. Sipanakhale konse nthawi yomwe Mulungu anayamba watenga konse chipembedzo, napanga chitsitsimutso kuchokera mwa icho, palibe paliponse. Ndiye, kupyolera mu mbiriyakale ndi mwa Baibulo, zikutsimikizira kuti ndi chinthu chauve pamaso pa Mulungu, kotero ine sindikufuna kalikonse kochita ndi izo. Ndipo ndicho chifukwa ine ndikuzitsutsa. Ine ndikuyesa kuwatenga anthu achoke ku izo.

⁶¹ Ife ndife oyitanidwa, monga mu Israeli, kotero izo zirinso tsopano, kuti tiziyang’ana kwa Israeli monga zitsanzo. Iwo, nthawi yonse iwo amakhala ndi Kasupe ameneyo, iwo anali onse bwinobwino. Koma pamene iwo anafika pa kudziwolera okha zitsime, kachitidwe kopangidwa ndi anthu, ndiye Mulungu anawasiya iwo ali phwathalala. Iye adzatichita ife mofanana.

“Two anali atamusiya Iye, Kasupe wa Madzi amoyo.” Awo anali madandaulo amene Mulungu anali nawo mowatsutsa iwo. “Kuti apange chinachake chimene iwo akanakhoza kunena, ‘Inu mukuona zomwe ife tachita!’”

⁶² Tsopano, pamene mu nthawi ya—ulendo wa Mose; pamene Mulungu, mwa chisomo, anali atawapatsa iwo mneneri, anali atawapatsa iwo Lawi la Moto kuti lizipita patsogolo pawo, anali atalitsimikizira Ilo mwa zizindikiro ndi zodabwitsa. Chisomo chinali chitapereka zinthu zonse izi. Israeli anali akufunabe, anawona lamulo. Iwo anachikana chisomo, kuti atenge lamulo.

Ndizo chimodzimodzi zimene anthu akuchita lero. Iwo akuwakana Mawu, kuti atenge kachitidwe ka chipembedzo, chifukwa mmenemo iwo akhoza kuchita zimene iwo akufuna kuchita ndi kumadutsa nazo izo. Koma inu simungakhoze kuchita izo mwa Khristu! Inu muyenera kubwera woyera ndi poyera, polinga kuti mukhale mwa Khristu.

⁶³ Kusiya chitsime chakasupe, pofuna kachitidwe kopangidwa ndi munthu kapena chitsime, kodi inu mungakhoze kulingalira winawake akuchita izo? Kodi inu mukanakhoza kulingalira zikholidwe za ubongo wa munthu yemwe akanakhoza kumwa pa chitsime cha kasupe wozizira, ndipo akanachisiya icho chifukwa cha chitsime chopangidwa ndi munthu chokhala ndi achule, ndi abuluzi, ndi mbululu, ndi china chirichonse mwa icho?

Izo siziri kuwoneka ngakhale mwanzeru kuti zikhale zolondola, koma ndizo chimodzimodzi basi zomwe anthu achita. Iwo awasiya Mawu, Kasupe woona wa gwero la Mulungu ndi Mphamvu, kuti azimwa kuchokera ku zitsime, ndi kudzipangira okha zitsime. Momwemo monga iwo anachita apo, iwo azichita izo tsopano. Iwo akuti. . .

Iye anati, “Iwo andisiya Ine.” Apa Iye anati, apa mu Yeremiya 2:14, kapena 13, kani. Iye anati, “Iwo andisiya Ine, Kasupe wa Madzi amoyo.”

⁶⁴ Tsopano, ife tikuwona chomwe chitsime chiri. Ife tikuwona chomwe icho chimagwira. Ife tikuwona momwe icho chimapangidwira. Ndi chinthu chopangidwa ndi munthu chimene chimabwera kuchokera pa denga lonyansa. Madzi amene amagwera pansu, amamenya pa denga lonyansa, ndipo iwo amangolitsuka dengalo, kuwagwetsera iwo pansu kupyolera mu chodzeretsa chopangidwa ndi munthu, kupyolera mu chotsanulira chopangidwa ndi munthu, kupita mu thanki lopangidwa ndi munthu. Ndipo nyansi zonse zimasonkhana mmenemo, ndi—majeremusi, ndi abuluzi, ndi achule, ndi zinthu za pa mtunda, zimakonda zimenezo. Ndipo, zindikirani, izo ziri nyama yosayera; mbululu, chithaphwi. Mbululu siyingakhoze kukhala mu madzi oyera. Ngati iyo itero, iwo akhoza kuyipha iyo. Iyo iyenera kuti izikhala mu madzi achithaphwi.

⁶⁵ Ndipo ndi momwe ziriri ndi ambiri awa apheterere lero. Inu simungakhoze kukhala moyo mu madzi atsopano a Mzimu Woyera. Ndicho chifukwa iwo ali molimba chotero potsutsa Mawu, ndi kunena, “Iwo amadzitsutsa Okha. Palibe kanthu kwa Iwo.” Ndi chifukwa chakuti iwo ayenera kukhala ndi mtundu wina wa dziwe lachithaphwi kuti azizunguliramo. Kulondola.

Ndiyo njira yomweyo iliri ndi achule, ndipo ndi abuluzi, ndipo ndi ananchidwe, ndi zonga zimenezo. Izo ziyenera kuzungulira pa dambo kapena dziwe lachithaphwi, kuti zizikhalamo, pakuti ndicho chikhalidwe chake kuti zizikhala mmenemo. Ndipo inu simungakhoze kuyisintha nyama mpaka inu mutasintha chikhalidwe chake.

Ndipo inu simungakhoze kumupanga munthu kuwona Mawu a Mulungu mpaka chikhalidwe chake chitakhala chitasinthidwa; ndipo pamene chikhalidwe chake chasinthidwa kuchoka ku chimene iye ali, kukhala mwana wa Mulungu, ndipo Mzimu Woyera umabwera mwa iye. Mzimu Woyera unalemba Mawu a Mulungu!

⁶⁶ Lero ine ndinali kuyankhula ndi mzanga wabwino, Doctor Lee Vayle, yemwe alipo tsopano. Ndipo iye ndi wazamulungu ndithu, ndipo kotero ife kawirikawiri timakhala ndi zina—timakhala ndi zokambirana zina zabwino kwambiri pa Lemba. Wophunzira kwambiri.

Ndipo iye anandifunsa ine nthawi yina chomwe ine ndinkaganiza za umboni weniweni wa Mzimu Woyera, “Kodi iwo unali kuyankhula mu malirime?” Izo zakhala ziri zaka zambiri zapitazo.

Ine ndinati, “Ayi; sindingakhoze kuziwona izo.”

Iye anati, “Ngakhale ine sindikutero,” anati, “ngakhale ine ndakhala ndikuphunzitsidwa izo.” Iye anati, “Inu mukuganiza kuti umboni wake ukanakhala chiyani?”

⁶⁷ Ine ndinati, “Umboni wangwiro kwambiri umene ine ndingakhoze kuwuganizira uli chikondi.” Ndipo kotero ife tinayamba kuyankhula pa icho.

Ndiyeno ine ndinaganiza izo zikumveka bwino kwambiri kotero ine ndinangogwirizira chimenecho, “Ngati munthu ali nacho chikondi.”

Koma tsiku lina Ambuye, mu masomphenya, anandiwongola ine pamenepo. Ndipo Iye ananena, kuti, “Umboni wa Mzimu unali iwo amene akanakhoza kulandira Mawu,” osati chikondi, kapena kuyankhula mu malirime, koma ndi kulandira Mawu.

⁶⁸ Ndiyeno Doctor Vayle anali kunena kwa ine, kuti, “Izo ziri Mwamalemba,” iye anati, “chifukwa, mu Yohane 14, Yesu anati, ‘Pamene Iye Mzimu Woyera abwera pa inu, Iye adzawulula zinthu izi kwa inu, zomwe Ine ndakuphunzitsani inu, ndipo adzakusonyezani inu zinthu ziri kudza.’”

Kotero pamenepo pali umboni weniweni wa Mzimu Woyera! Iye sanayambe wandiuzapo ine chirichonse cholakwika panobe. Iwo, “Uli umboni wa Mzimu Woyera, ndi iye yemwe angakhoze kukhulupirira Mawu, ngati inu mungakhoze kuwalandira Iwo.”

Chifukwa, Yesu sananene konse kuti, “Pamene Mzimu Woyera wabwera, inu mudzayankhula ndi malirime.” Iye sananene konse, kuti Mzimu Woyera ukabwera, inu mudzachita chirichonse cha zinthu zimenezo. Koma Iye anati, “Iye adzatenga zinthu Zanga izi ndi kuzisonyeza izo kwa inu, ndipo adzakusonyezani inu zinthu zimene ziri nkudza.” Kotero umenewo uli umboni weniweni wa Mzimu Woyera, malingana ndi Yesu Iyemwini.

⁶⁹ Kotero zogirigisha zonse izi ndi zinthu zomwe anthu ali nazo ndipo akukhala ali moyobe, inu mukhoza kuwona chifukwa chimene iwo amachitira izo. Mwaona, icho chimasandulika chipembedzo, kapena dziwe lachithaphwi, ndipo sipadzakhala pali chipembedzo chopangidwira pa kusa-. . . Mawu angwiro a Mulungu. Iwo sangakhoze kuchita izo, chifukwa inu simungakhoze kusankha kapena kumulamulira Mulungu. Ayi, bwana!

⁷⁰ Chifukwa chake chiri, inu mumatenga gulu la anthu amene angakhoze kukhulupirira Mawu, nkuwalola iwo kuti ayambitse bungwe. Chinthu choyamba inu mukudziwa, mu nthawi ya chaka pali gulu la Marike mkati mmenemo amene inu simungakhoze kuchita nawo kanthu. Iwo agwiritsitsa, ndipo inu simungakhoze kuchita kanthu nawo iwo. Si ndiko kachitidwe ka Mulungu. Iko si kali, kotero ife tikudziwa kuti chinthu chimenecho chiri kunja. Ichu chimakhala chitsime, ndipo amakhala malo amene aliyense ati azinyengerera pa *izi*, *izo*, kapena *chimzake*, kuti atengere mamembala mkati umo, kapena kulola anthu abwere mmenemo.

⁷¹ Ife tikupeza kuti, kachitidwe aka kanayambika nthawi imodzi, mmbuyo mu masiku a Aisreli, pamene iwo anali kukumba zitsime izi. Ndipo uko kunali munthu ndi gulu la Afarisi omwe anali atakumba zitsime zina. Ndipo iwo anali naye munthu wotchedwa Herodi, ndipo iye anali wolamulira, kazembe wa boma.

Ndipo iye anabwera pansu kudzamumvera munthu yemwe sanali kupusitsidwa ndi zipembedzo zawo. Iye anali mneneri. Ndipo palibe mneneri yemwe anayamba wakhalapo ndi chinthu chirichonse chochita ndi chipembedzo, koma ankadana nacho icho. Mneneri uyu anayamba kunena kuti, “Musati muyambe kunena mwa inueni, ‘Ife tiri naye Abrahamu kwa atate athu,’ chifukwa Ine ndikukuuzani inu kuti Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu.”

⁷² Ndipo iwo anali atabweretsa wolemekezeka kuti akamumvetsere iye. Ndipo wolemekezeka uyu anali atalanda

mkazi wa m'bale wake kwa iye, ndipo iye anamukwatira iye. Ndipo kodi munthu ameneyo anayenda kupita pa nkhope yake ndi kukanena chiyani? Iwo ankaganiza kuti iye akananyengerera, ndi kunena, “Tsopano, bwana, inu, inu khalirani pokhala pabwino cha *apa*. Ndipo inu muyenera kuti . . . ine ndiri wokondwera kwambiri kuti inu muli pano kudzandimvera ine lero.”

Yohane anangoyenda mpaka pa nkhope yake, ndipo anati, “Si ziri zololeredwa kuti inu mukhale naye iye.” Chinthu choyamba chomwe chimene iye ananena, iye anamukalipira iye chifukwa cha tchimo lake.

⁷³ Mukuona, zipembedzo zimapanga madziwe azithaphwi mmene mwamuna angakhoze kumagona ndi akazi, ndipo akazi amenewo angakhoze kumapitiriza, ndi kumadula tsitsi lawo, ndi kumavala akabudula, ndi chinthu chirichonse, ndi kumadzitcha okha Akhristu.

Koma Kasupe weniweni, aleluya, wa Mphamvu ya Mulungu, izo sizingakhoze kukhala mmenemo, chifukwa Iye amakankhira izo panja. “Ine ndine Kasupe wa Madzi amoyo. Iwo andisiya Ine, kuti akadzikumbire okha zitsime zina.”

⁷⁴ Tsopano, kasupe wa madzi amoyo, ife tikupeza, kasupe wa madzi amoyo ndi chiyani? Ife tapeza chomwe chitsime chiri, tsopano kasupe wa madzi amoyo ndi chiyani? Ndi chitsime chakasupe.

“Chitsime chakasupe, ndi chiyani chimenecho, M'bale Branham?”

Ndi chitsime chomwe chiri nthawizonse amatuluka kuchokera pansi ndi kumakankhira madzi ake kunja. Ndi oyenda nthawi zonse. Icho chimadzithandiza chokha. Nthawizonse ozizira ndi oyera, chitsime chakasupe, kasupe wa madzi amoyo. Iye sali wakufa ndi wovunda. Iye ndi wamoyo, iye ndi wosinthasintha nthawizonse, kubweretsa chinachake chatsopano nthawi zonse, kumasunthabe patsogolo, kumabwera kuchokera ku magwero ake. Iye amakoka magwero ake kuchokera—kuchokera ku kama wake, yemwe ali . . . akadali kasupe wa madzi amoyo akutumphukira mmwamba. Odziyetsa-okha; ndi oyera, angwiro, madzi oyera. Ndi odzithandiza-okha; inu simumasowa kuti muyembekezere mvula kuti idzazitse thanki yake. Iye nthawizonse amabubulikira mmwamba, amapereka madzi ake mwaulere. Inu simusowa kuwapompa iwo, kuwapukusa iwo, kuwapotokola iwo, kapena kuwajowina iwo. Ndi kasupe basi wa madzi amoyo.

⁷⁵ Inu mukudziwa, inu mukatenga zitsime zakale izi, inu mumasowa kumazipukusa izo ndi kuzipukusa izo ndi kuzipukusa izo, ndi kuwampopa ndi chirichonse, kuti mupangitse pang'ono a madzi achithaphwi awo atuluke. Nha!

Koma Kasupe wa Madzi amoyo amapereka Iwo kunja, mwaulere, popanda kupompa, kujowina, chinthu chirichonse. O, ndine wokondwa chifukwa cha Kasupe ameneyo! Inde, bwana!

⁷⁶ Iye samasowa sefa pa Iye, kuti muchotse tapheterereto titulukemo. Pakuti, Iye akuchokera pansi mwakuya kwambiri, mmenemo mu Thanthwe, mpaka mulibemonso tapheterere mmenemo.

Iye sasowa kukhala ndi chiguduli cha maphunziro chitapachikidwa pa Iye, ndiko kulondola, kachitidwe kena kopangidwa-mwachidziko ka nzeru za chipembedzo zopangidwa ndi munthu; kuti akuuzeni inu, pamaso pa wopima misala, ngati uli wokhoza kuti uzilalikira kapena ayi. Iye alibe chimodzi cha ziguduli zauve izo zitapachikidwa pa Iye. Iye akanazikankhira izo kumbali kumene mwamsanga pamene inu mukanayika icho pamenepo. Inu simungakhoze kuchita izo. Chitsime chimenecho chikububulika, nthawi zonse. Inu mukhoza kuyika chimodzi cha ziguduli izo pa iye, iye akanakachinkhira icho kunja kumbali imodzi kapena imzake. Iye alibe nthawi imodzi ya chiguduli cha chipembedzo pa iye.

⁷⁷ Iye sasowa chotchezera ayi, sefa ayi, kupompa ayi, kugwedeza ayi, chinthu chirichonse ayi. Ali pamenepo basi, akububulikira mmwamba. Iye sasowa kuti azidalira pa mvula wamba kuti imudzazitse iye. *Mvula* ndiyo “zitsitsimutso,” kumene Kasupe ameneyo...Ndiko ku Kasupe wa Moyo ameneyo. “Kumene kuli Nyama, mphungu zikasonkhanako.” Inu simusowa kupompa chitsitsimutso; inu simusowa kupompa chirichonse. Chinthu chokha chimene inu muyenera kuchita ndi kungobwera ku Kasupe. Iye nthawizonse amakhala wodzaza ndi madzi abwino, ozizira, ndipo palibe mathero kwa Iye. Iye amangopitirirabe kutumphuka.

⁷⁸ Inu simusowa kupita ku chitsime, ndi kukati, “Chabwino, ngati iti ivumbe ndi kutsuka pa baraniyo, ife tikhala ndi chinachake choti nkumwa.” Mwaona? Mai, mai! Osati uyu. Chitsime cha kasupe uyo chiri kuwatulutsa madzi abwino, ozizira nthawi zonse. Inu mukhoza kudalira pa iye. Inu simusowa kuti, “Chabwino, ine ndipita ku chitsime chakale ichi. Ife tinali kumwa pa icho, koma kuti iyo sinavumbe kwa nthawi yaitali. Ine ndikukuuzani inu, icho chikhoza kukhala chitawuma.”

⁷⁹ Ndimo momwe ena a machitidwe opangidwa ndi anthu awa aliri. Inu mukhoza kulowa mkati, ngati inu muli ndi china chiri chachikulu chikuchitika, mwambo wawukulu wachinsinsi wogulitsa chinachake, kapena—kapena mtundu wina wa chinachake chikuchitika, maphwando akuluakulu ndi zinthu zikuchitika, masewero amatsenga, ndi maphwando mu chipinda cha pansu, ndi chirichonse, inu mukhoza kupeza nyumba itadzaza.

Koma pamene inu mupita kumene Kasupe uyo akutumphukira, nthawizonse, anthu ali kumeneko akumwa madzi abwino, ozizira. Inu mukhoza kudalira pa Iye! Mukuti, “Iwo sanakhale ndi chitsitsimutso kwa zaka khumi” Ngati inu mukhala moyo mwa Kasupe ameneyo, Iye nthawizonse amakhala nacho chitsitsimutso chiri kuchitika.

⁸⁰ Monga bambo wachi Welshi wamng’ono ananena. Kapena, nthawi yina pamene iwo anali ndi chitsitsimutso chachi Welshi chiri kuchitika, uko kunali olemkezeke ena ochokera ku States. Ena a Madokotala aakulu awa a Zauzimu anapita ku Wales komweko, kuti akapeze malo ake ndi chomwe zonse izi zinali. Koteri iwo anali atavala makolala awo otembenezidwa, ndi zipewa zawo zosomeka, ndipo iwo anali akuyenda pansu mu msewu.

Ndipo apa panabwera msirikali wamng’ono motsatira, akuzunguza ndodo yake yayifupi yaying’ono mu dzanja lake, akuyimba muluzi, “Pansi pa mtanda pamene Mpulumutsi wanga anafera, pansu apo kuti nditsukidwe kuchoka ku tchimo ine ndinalira; pamenepo kwa mtima wanga Magazi anapakidwa, ulemerero ku Dzina Lake,” akuyenda pansu mu msewu.

Koteri iwo anati, “Uyu akuwoneka ngati munthu wachipembedzo. Iye tipita tikamufunse iye.”

Ndipo iwo anati, “Bambo!”

Anati, “Eee, bwana?”

Iye anati, “Ife tiri kuno kuchokera ku United States. Ife ndife nthumwi. Ife tabwera kuno kuti tidzafufuze chitsitsimutso cha Welshi, chotchedwa-choncho. Ife ndife Madokotala a Zauzimu, ndipo tiri pano kuti tidzayang’ane bwino pa icho.” Iye anati, “Ife tikufuna kuti tidziwe kumene kuli chitsitsimutsocho, ndi komwe icho chikuchitikira.”

Iye anati, “Bwana, inu mwafika. Ine ndine chitsitsimutso cha Welshi.” Amen! “Chitsitsimutso cha Welshi chiri mwa ine. Pano ndi pamene icho chiri.”

⁸¹ Ndi momwe izo ziriri pamene iwe ukhala moyo mwa Kasupe wa Madzi amoyo uyo. Iye amakhala wamoyo nthawi zonse, akutumphuka mobwereza bwereza, ndi mobwereza bwereza. Palibe mathero kwa Iye. Osati, “Pitani mukawone ngati madzi ena, ngati ife tinali ndi mvula kuno osati kale litali,” si ndizo izo. Ndi Kasupe wa Madzi amoyo uyo. Monga ine ndikuti, Iye amapereka Madzi Ake mwaulere.

⁸² Inu simusowa kuyika ziguduli pa Iye, kuti mufufuze apo; ziguduli zina za maphunziro, musanati mumutumize iye kunja kuti azikalalikira, ndi kuwona ngati iye akutchula mawu ake molondola, kuwayankhula iwo molondola, ngati iye akugwiritsa ntchito manauni ake ndi mapuronauni, ndi zina zotero, ndi

afotokozi. Ambiri a iwo sadziwa nkomwe chomwe izo ziri, koma iye akukhala pa Kasupe mofanana basi, mwaona, mofanana.

⁸³ Iye sachita kuti azidalira pa mvula wamba, kuti imudzadzitse iye, kapena zitsitsimutso wamba, kwa iye. Iye sasowa kuchita zimenezo, pakuti Mphamvu yake ndi chiyero chake ziri mkati mwa iyeyekha. Ndiko kumene Mawu ali, Mphamvu Yake Yomwe! Pamene munthu angakhoze kuwalandira Iwo mu mtima wake, Iwo ali nacho chiyero Chake. Iwo ali nayo mphamvu Yake. Izo ziri mu Mawu Omwe kumene, akutumphukira apo ku Moyo.

⁸⁴ Israeli akachoka kwa Iwo, iwo amalowa mu vuto. Nthawi iliyonse imene iwo amachoka kwa Iwo, iwo ankalowa mu vuto.

Zofanana monga ife tikuchitira tsopano. Pamene chitsitsimutso chichoka kwa Iwo, ndiye izo siziri zabwino. Iye amadzikumbira yekha zitsime zina, ndi, kapena zitsime zina zazithaphwi, ndipo apo icho chimapita.

⁸⁵ Koma Iye nthawizonse ankawathandiza iwo. Kung'ung'uzo pa Nyanja Yofiira, ndiye pamene iwo anang'ung'uzo... Komabe, mu zonse izo, Iye anali atawalonjeza, anali atawapangira iwo lonjezo. Iye akadayenera kuwakana iwo kumbuyo komwe uko, momwe ife tikanayang'anira pa izo; koma Iye anali atawalonjeza kuti awatengera iwo kutsidya uko.

Kodi Iye anachita chiyani? Ana a Israeli aja, Iye anawapatsa iwo Lawi la Moto ndi chirichonse, mwa kutsimikizira, mneneri wawo. Ndipo iwo anawatsogolera iwo kumeneko kupita ku nyanja. Ndipo, nthawizonse, pamakhala vuto lotsutsa Iwo. Ndipo apa panabwera Farao ndi ankhondo ake. Ndipo inu mukudziwa chimene Mulungu anachita? Iye anangochitsegula chitsime chofiira, chachithaphwi chija.

Nyanja Yakufa ili chinthu chakufa kwambiri mu dziko. Ili yakufa kwenikweni. Ndi yachithaphwi. Palibe chingakhoze kukhala moyo mwa iyo.

Ndipo Iye anayitsegula iyo ndi kuwamasula iwo mfulu, ku mbali inayo. Iye anawatengera iwo kupita komwe sakanati azikakhala ali omangidwa ndi chinthu chotero monga icho.

⁸⁶ Mu chipululu, iwo anapeza kuti mathanki sakanakhala woti akamadalaridwa; iwo anali atawuma. Tinapeza kuti, iwo ankapita kuchokera ku dzenje limodzi la madzi kupita ku limzake. Pamene iwo anali mu chipululu, iwo anali kuzunzika mwapafupi kufa, chifukwa cha madzi akumwa. Ndipo iwo amakhoza kupita ku thanki iyi cha apa, dziwe; ilo linali litauma. Iwo amapita ku malo ena; ilo linali litauma. Iwo sakanakhoza kuganiza basi kuti iwo akanapeza konse oti amwe.

Ndiyeno pa malo osayembekezeka kwambiri mu chipululu chonse, iwo anapezapo madzi. Iwo anali mu thanthwe. Iwo anali mu thanthwe. Malo osayembekezeka kwambiri omwe munthu

akanapeza madzi aliwonse, akanakhala mu thanthwe lowuma pakati pa chipululu. Koma, inu mukuona, Mulungu amachita zinthu monga choncho. Mu malo osayembekezeka kwambiri, mwa njira yosazolowereka kwambiri. Ndicho chimene ife takhala nacho nthawizonse.

⁸⁷ Iwo amaganiza kuti iwe uyenera kuti ukhale ndi zipembedzo zazikulu, palimodzi, ndi kuwalola iwo onse abwere palimodzi ndi kukhala ndi chipiringu chachikulu pozungulira, ndi zina zotero, ndi kutenga zikwi kuti agwirizane, ndi zonse monga *zimenezi*, kuti ukhale ndi chitsitsimutso.

Nthawizina Mulungu amamutenga munthu wamng'ono wachikulire wosadzija konse ABC wake, ndipo pakati pomwe pa gulu la anthu osaphunzira omwe sadziwa nkomwe dzanja lawo lamanja kuchokera kumanzere, Iye akhoza kudzutsa chitsitsimutso chomwe chiti chigwedezze dziko. Iye anachita izo mu nthawi ya Yohane. Iye anazichita izo mu nthawi ya aneneri. Palibe wa iwo, monga ife tikudziwira, anakhala wophunzira, koma Mulungu amakhoza kufika powatenga iwo ndi kuchita chinachake ndi iwo.

⁸⁸ Mu Thanthwe ili munatulukamo madzi. Iye anali Thanthwe. Ndipo Iye analamulira Thanthwe ili, ndipo liyenera kuti likanthidwe. Ndipo Iye anapereka yunjinji wa madzi angwiwo, atsopano, overa kwa aliyense yemwe akanati amwe. Iye anapulumutsa onse amene akanati amwe ochokera mwa Ilo. Chofanana changwiwo ndi Yohane 3:16.

...Mulungu anakonda dziko kwambiri, kuti iye anapereka Mwana wake yekhayo wobalidwa, ... aliyense yemwe akhulupirira pa iye asati awonongeke, koma akanati akhale nawo moyo wosatha.

⁸⁹ Mulungu anakantha Thanthwe limenelo, pa Gologota. Chiweruzo chathu chinali pa Iye, kuti kuchokera kwa Iye kukakhoze kubwera Mzimu wa Moyo umene ukanati ukupatseni inu ndi ine Moyo Wamuyaya. Ndilo fanizo langwiwo la Ilo, uko mu chipululu ichi.

⁹⁰ Iwo sankasowa kuti azikoka, kukumba, kupompa, kapena chirichonse; kungotenga nawo za njira Yake yoperekedwa, mwaulere. Pamene, iwo sankasowa kuti aziwakumba iwo kuchokera mu dziwe. Iwo sankasowa kuti aziwakoka iwo ndi chibekete. Iwo sankasowa kuti achite kupukusa kuti awatunge iwo nako. Iwo ankangoyenera kuti atenge nawo a ilo.

Ndipo ndizo zonse ziripo tsopano. Inu simusowa kuti mujowine kanthu. Inu simusowa kuti mubwere pansu pa guwa ndi kudzichititsa chinachake, kuchipompa icho. Inu simusowa kuti munene mawu mobwereza ndi kubwereza bwereza, mpaka inu mukhale ndi chisokonezeko cha chiyankhulo. Chinthu chokha chimene inu muyenera kuchita ndi kungotenga nawo za Iye, mwaulere, njira yoperekedwa ndi Mulungu. Popanda

kupompa, popanda kukankha, popanda kalikonse; kungotenga za Iye, mwaulere. Palibe kanthu kamene inu muyenera kuchita; kungotenga za Iwo. Uko ndi, kuwakhulupirira kokha Iwo. Ndizo zonse zomwe Ine ndingakhoze kunena kwa izo.

Iwo sankasowa kuti achite kalikonse kwa izo. Osati kuti uchite kukumba pofuna iwo. Iwo sankasowa kuti akhale pansi ndi kulira usiku wonse, pofuna iwo. Iwo ankangotenga za iwo; ilo linali litakanthidwa ndi lokonzeka. Ndiko kulondola.

⁹¹ Ine ndikuyang'ana pa mwamuna tsopano, wakhala mmbuyo mu chipinda chino. Ine ndikukumbukira ndikumuuza iye izo, pa nyumba ya barani yakale tsiku lina, pambali pa khola.

Ndipo iye anati, “Koma sindine wabwino.”

⁹² Ine ndinati, “Ine ndikudziwa kuti inu si muli.” Ndipo ine ndinati, “Ine sindiri, ngakhale.” Koma ine ndinati, “Inu mukuyang'ana pa chomwe inu muli. Ndipo siyani kuyang'ana pa chomwe inu muli, ndipo penyani chomwe Iye ali.”

Iye anati, “Ngati ine ndikanangoti ndisiyane nazo ndudu izi, M'bale Branham, ine—ine—ine ndikanakhala Mkhristu.”

⁹³ Ine ndinati, “Musati musiyane nazo izo. Inu mukuyesera kuti mukhale wabwino ndipo kenako mubwere kwa Iye. Iye sanabwere konse kuti adzapulumutse munthu wabwino; Iye anabwera kuti adzapulumutse munthu woyipa omwe ankawadziwa iwo anali oyipa.”

Iye anati, “Chabwino . . .”

Ine ndinati, “Mvetserani, inu simukufuna kuti mupite ku gehena, mukufuna inu?”

Iye anati, “Ayi.”

⁹⁴ Ine ndinati, “Chabwino, inu simukusowa kutero. Iye anafa kuti inu musachite kuti mupiteko.”

Iye anati, “Kodi ine ndikusowa kuchita chiyani?”

Ine ndinati, “Palibe. Ndi zophweka basi chotero.”

Iye anati, “Koma ngati ine ndikanakhoza konse . . .”

⁹⁵ Ine ndinati, “Apo inu mukupita, kubwerera ku ndudu ija kachiwiri. Siyani kuganizira za ndudu imeneyo. Ingokumbukirani, ganizani za Iye, chimene Iye anachita, chimene Iye ali; osati chimene inu muli. Inu si ndinu wabwino; ndipo inu simunakhalepo muli, ndipo simudzakhala muli konse. Koma, chomwe Iye ali, Iye ndiye Mmodzi!” Ndipo ine ndinati, “Tsopano, chinthu chimodzi chokha chimene inu muyenera kuchita; ngati Iye anatenga malo anu pansu uko, inu mololera basi landirani chimene Iye anachita. Chinthu chokha chimene inu muyenera kuchita ndi kungozilandira izo.”

“Bwanji,” iwo anati, “izo nzophweka. Ine ndichita izo.”

⁹⁶ Ine ndinati, “Apa pali mtsinje.” Mwaona? Ine ndinawabweretsa iwo kuno ndi kuwabatiza iwo mu Dzina la Yesu Khristu.

Ena abale ake ali pano, ndipo ine—ine ndikudziwa kuti iwo anamverera mwachirendo ndi ine chifukwa chochita izo, koma ine ndinkadziwa chimene ine ndinali kuchita. Ine ndinawona mwa munthuyo chinachake chimene chinali chenicheni. Ine ndimakhoza kuchiwona icho mmenemo, ndipo ine ndinamutenga iye ndi kumubatiza iye mu Dzina la Ambuye Yesu.

Ndipo, pamene ife tinachita icho, sizinali motalika zitachitika izo mpaka ine nditapita ku nyumba ya mwana wake. Ife tinawona ma—masomphenya a mtengo ukuthyoka pa malo ena, ndipo munthuyo anagwa, pafupifupi kuthyola nsana wake. Tinamutengera iye ku chipatala. Ndipo usiku umenewo Ambuye anaulula, kwa ine, kuti amenewo anali mapeto a ndudu.

Kotero tsiku lotsatira iye ankafuna ndudu zina. Ine ndinati, “Ine ndimugulira iye ktoni ndi kulitengera ilo kwa iye. Inu mungoyang’ana ndi kuwona, masiku ake a ndudu anali atatha.” Iye sanasuteponso imodzi kuchokera apo, ndipo samafunanso imodzi kuchokera apo. Mulungu!

⁹⁷ Mwaona, chinthu choyamba chimene inu muyenera kuti muchite ndi kubwera ku Kasupe ameneyo. Inu muyenera kubwera ku Madzi amenewo, kuzindikira si chinthu chimene inu mungakhoze kuchita. Ndi chimene Iye anakuchitirani kale inu. Inu simusowa kukumba; inu simusowa kupompera kunja; inu simusowa kusiya *izi*; inu simusowa kusiya *izo*. Chinthu chokha chimene inu muyenera kuchita ndi kufika pamenepo ndi kumwa. Ndizo zonse. Ngati muli waludzu; imwani!

⁹⁸ Tsopano, Iye anali Thanthwe. Mulungu anamukantha Iye chifukwa cha ife, ndipo Iye anapereka kuchuluka kwa madzi angwirowo, oyera. Iye akuchita panobe, lero, kwa aliyense yemwe ati akhulupirire. Ichi ndi chisomo Chake, ndithudi, kwa anthu Ake, ife.

⁹⁹ Pali chinachake chonga pamenepo, monga anthu a lero, okonzeka kuti alandire chimene iwo angakhoze kupeza, koma samafuna kuti apereke kutumikira kulikonse mwa kubwezera. Israeli anali wokonzeka kuti—kuti amwe kuchokera ku thanthwe tsopano, koma iwo sanafune kuti amupatse Mulungu kutumikiridwa Kwake komwe kunali koyenera Iye.

¹⁰⁰ Ndipo Iye nthawizonse ali kumatipatsa ife kutumikira. Inu mukudziwa, ife sitingakhoze ngakhale kupuma popanda Iye. Ife sitingakhoze kupuma popanda kutumikira kwa Mulungu. Ndimomomwe ife tiriri odalira pa Iye. Ndipo, komabe, izo pafupifupi zimatiswa ife pawiri ngati ife tiyesa kuti tichite, kuti tichitire chinachake kwa Iye. Iye akatifunsa ife kuti tichite chinachake, pitani kuti mukamuwone winawake,

pitani mukamupempherere winawake, pitani mukamuthandize winawake, izo pafupifupi zimatiswa ife, kuti tizichite izo. Koma ife sitikufuna kuti tichite chirichonse kwa Iye mwa kutumikira.

¹⁰¹ Dandaulo lake linali, “Iwo andisiya Ine, Mawu; ndipo avomereza chitsime chong’aluka, mmalo mwake. Kuvomereza . . . Iwo andisiya Ine, Kasupe wa Moyo, Kasupe wa Madzi a Moyo; ndipo iwo akukhumba ndipo kulibwino kuti amwe kuchokera ku chitsime chachithaphwi.” Kodi inu mukanakhoza kulingalira zimenezo?

¹⁰² Kodi inu mukanakhoza kulingalira munthu tsopano, yemwe, *pano* pali chitsime cha kasupe akungotulutsa kunjwa iwo madzi abwino aja, a mwala wa laimu, kuchokera mu mtima momwe mwa matanthwe, pansu apo mu khoma la mchenga, ndi zina zotero, basi ozizira ndi abwino monga iwo akanakhoza kukhalira; ndipo kulibwino iwo amwe kuchokera mu chitsime cha ukocho, chomwe chinali chitatsuka pa denga la barani, ndi mashedi, ndi zonse za kunjwa kwa manyumba pozungulira malowo? Ndi kuziyika izo kumene mu chitsime chimenecho apo, mipita ya madzi imabweretsamo kumene, kuchokera ku barani, ndi makola ndi mosungiramo, ndi chirichonse kutsanuliranso mu chitsimecho, basi ndiyeno ife tikufuna kula- . . . tikanati timwe kuchokera mmenemo ife tisanapite ku chitsime cha kasupe? Pakhoza kukhala pali chinachake chitalakwika mwaubongo ndi munthuyo. Ndiko kulondola.

¹⁰³ Ndipo pamene mwamuna kapena mkazi ati atenge chipembedzo pa kuyima kwawo, chomwe chiti chiziloleza tsitsi lodulidwa, kuvala zazifupi, zopakapaka, zinthu zonse za mtundu wina izi, ndi zina zazing’ono za mtundu wa pu—purogaramu, ndi zotengeka zonse izi, ndipo nkukhoza kumapita ku mabwalo amasewero, ndi—ndi zamkhutu zonse izo kunja uko, ndipo akhoza kumapitirira nazo izo; ndipo monga chomwecho bwinoko kuposa momwe iwo amachitira ndi Mawu a Mulungu a kachitidwe kachikale kamene kamadulira pansu ndi kubowola, ndi kupanga madona kuchokera mwa akazi, ndi kuwatenga ndi kuwapanga iwo kuvala bwino ndi kumachita mwabwino, kutenga ndudu ndi fodya, ndi kulumbira ndi kutukwana, ndi kunama ndi kuba, kutali zichoke kwa inu, ndi dziko lonse kutali ndi inu, ndi kukupatsani inu Chinachake chomwe chiri chokhutitsa mwangwiwo. Nchifukwa chiyani mwamuna kapena mkazi amapita ku chinthu chonga chimenecho pofuna chithonhozo? Iwe ungakhoze bwanji kupeza chithonhozo kuchokera mwa izo?

¹⁰⁴ Iwe ungakhoze bwanji kupeza chakumwa chamwatsopano kuchokera ku chitsime chachithaphwi? Munthu angachite bwanji. . . Ngati munthu apita ku chitsime chachithaphwi kuti akamwe madzi, pamene pali chitsime cha kasupe atatseguka bwinobwino, iwe ukananena kuti, “Pali chinachake chalakwika ndi malingaliro a munthu ameneyo.”

Ndipo ngati mkazi kapena mwamuna apita ku malo oterowo kuti akapeze chitonthozo, pali chinachake cholakwika mwauzimu ndi munthu ameneyo. Iwo sakuwafuna Mawu. Izo zikusonyeza kuti chikhalidwe chawo chikadali chule, kapena mbululu, kapena chinachake, ndiko kulondola, chinachake cha chikhalidwe chimenecho chomwe chimakonda dziwe lachithaphwi limenelo, chifukwa mtundu wa zinthu umenewo sungakhoze kukhala mu dziwe la Madzi-abwino. Iwo sungakhoze kuchita izo; ndi Madzi abwino. Iwo sungakhoze kuchita izo.

¹⁰⁵ Tsopano, dandaulo linali, “Iwo amusiya Iye.” Ndipo lero iwo achita chinthu chomwecho.

Tsopano yang'anani pa mkazi wa pa chitsime. Chabwino, iye anabwera ku chitsime cha Yakobo, ndipo iye anali akutunga madzi kumeneko nthawi zonse, pa chitsime cha Yakobo. Koma chitsime cha Yakobo, chipembedzo, ife tikhoza kuchitcha icho, chifukwa iye anakumba zitatu za izo; ndipo chimodzi ichi chimene iye anali atachikumba. Tsopano, iye anali ndi nkhani yayikulu. Iye anati, “Tsopano, atate athu anakumba chitsime ichi, Yakobo. Iwo ankamwa kuchokera mu icho, ndipo ng'ombe zawo zinkamwa kuchokera mu icho, ndi chirichonse. Kodi zimenezo si zabwino mokwanira?”

¹⁰⁶ Iye anati, “Koma madzi amene iwe ukutunga kuchokera mmenemo, iwe umamvanso ludzu, umayenera kubwereranso kuno kuti udzawatunge iwo. Koma,” anati, “Madzi amene Ine ndikupatsa iwe ali Kasupe, Kasupe akutumphukira mmwamba kuchokera mkati, ndipo iwe sumabwera kuno kuti udzawatunge Iwo. Iwo amakhala ndi iwe kumene.”

¹⁰⁷ Zindikirani. Koma pamene iye anapeza kuti Kasupe wa Mwamalemba anali atayankhula kwa iye, mwa chizindikiro cha Mwamalemba chimene iye anakhala akuchiyembekezera, iye anasiya kachitidwe ka chipembedzo ka Yakobo kaja ndipo sanabwerere kwa iko kachiwiri, chifukwa iye anali atapeza Thanthwe lenileni. Mwaona? Iye anathamangira mu mzinda. Iye anali atathana nalo tchimo. Iye sanalinso mkazi woyipa. Iye anati, “Bwerani, mudzamuwone Yemwe ine ndamupeza, Munthu Yemwe wandiuzza ine zinthu zimene ine ndachita. Kodi sali Uyu Khristu amene?” Iye... Chitsime chimenecho chikanakhoza kukhala chabwinobwino; icho chinali chitatumikira cholinga chake. Tsopano iye anali pa Kasupe woona. Chitsime chinali chabwino kufikira pamene Kasupe woona anali atatsegulidwa. Koma pamene Kasupe woona anabwera motsatira, chitsime chinataya mphamvu yake. Iye anapeza kuti alipo malo abwinoko kumakamwa.

¹⁰⁸ Ndipo alipo malo abwinoko. Alipo malo abwinoko, ndipo ndimo mwa Khristu. Mu Yohane Woyera 7:37 ndi 38, Yesu ananena, pa mapeto a phwando la makachisi, “Ngati

munthu aliyense amva ludzu, mloleni iye abwere kwa Ine, ndi kudzamwa.”

Iwo anali onse akusangalala. Iwo anali nako kutumphuka kwapang’ono kwa madzi akubwera kuchokera pansi pa guwa, ndipo—ndipo pamenepo iwo anali onse kumwa kuchokera kwa awa, mu chisangalalo, cha—cha phwando. Ndipo anati, “Makolo athu anamwa kuchokera ku thanthwe lauzimu mu chipululu.” Mwaona, iwo anali atadzibowolera okha chitsime, madzi ena apachithaphwi omwe iwo anawapompa kuchokera kwinakwake, ndi kumawatsanulira iwo pansi pa kachisi apo. Ndipo iwo onse amafika pozungulira madzi awa ndi kumamwa, ndi kunena, “Zaka zapitazo, makolo athu anamwa mu chipululu.”

Yesu anati, “Ine ndine Thwanthe limenelo lomwe linali mu chipululu.”

Anati, “Ife tinkadya manna ochokera Kumwamba, ndipo Mulungu ankawavumbitsira iwo pansi.”

¹⁰⁹ Anati, “Ine ndine Manna amenewo.” Iye, Kasupe ameneyo, anali atayima pakati pawo. Mkate uja wa Moyo unali utayima pakati pawo.

Ndipo komabe iwo sanamufune Iye. Iwo kunali bwino akhale ndi chitsime chawo; chifukwa, munthu anali atapanga *ichi*, ndipo Mulungu anali atawatumiza Awo. Ndizo chimodzimodzi kusiyana kwake. Anadzikumbira wokha zitsime!

¹¹⁰ Iye anati, “Ngati munthu aliyense amva ludzu, mloleni iye abwere kwa Ine, ndipo amwe.” Iye ali Kasupe ameneyo.

Ndipo monga Lemba lanena, “Kuchokera mu chifuwa chake mudzasefukira mitsinje ya Madzi amoyo.” O, Iye ali chitsime cha kasupe chimenecho! “Kuchokera mu chifuwa chake, kapena mkati mwenimweni, mudzasefukira mitsinje ya Madzi amoyo.”

¹¹¹ Iye ali Thanthwe limenelo lomwe linali mu . . . Lomwe linali Thanthwe la Hagara, mu nthawi ya vuto; pamene mwana wake anali pafupi kuti afe, pamene iye anali atasiyidwa kunjwa kwa msasa, ndipo anali kunjwa uko ndi Ishmaeli wamng’ono. Madzi ake, mu chitsime chake chimene iye anali kuchinyamula, anali atatha. Ndipo iye anamugoneka Ishmaeli wamng’ono pansi; ndipo anayenda kupita, mtunda wa kuponya kwa uta, ndipo analira, ndipo, o, chifukwa iye sankafuna kuti amuwone mwanayo akufa. Ndipo zonse mwadzidzidzi, Mngelo wa Ambuye anayankhula, ndipo iye anapeza Beer-Beersheba, chi—chitsime kumeneko chomwe chinali kusefukira, ndipo chikanali kusefukira mpaka mu tsiku lino. Iye anali Beer-Beersheba wa Hagara, Thanthwe kunjwa kuja mu chipululu.

¹¹² Iye anali kuyima apa mu Kasupe wodzaza ndi Magazi, tsiku lija, atayima pamenepo mu kachisi. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . nthawi ya nkuntho. Mu Zakariya mutu wa 13, Iye anali Kasupe ameneyo wotseguka mu nyumba ya Davide,

kwa kuyeretsa, ndi kwa (tchimo) kuyeretsa kwa tchimo. Iye anali Kasupe ameneyo. Ndipo mu Masalmo 36:9, Iye anali Kasupe wa Moyo wa Davide. Iye akadali Kasupe ameneyo mu nyumba ya Davide.

Ndipo Iye ndi wandakatulo, mu mtima wake uko. Wandakatulo anati:

Pali Kasupe wodzaza ndi Magazi,
 Otengedwa kuchokera mu misempha ya
 Emanuele,
 Pamene ochimwa agwera mkati mwa
 kusefukirako,
 Amataya banga lonse la kuchimwa kwawo.

Iye ali Kasupe ameneyo wa Moyo, Kasupe wa Madzi. Iye ali Mawu a Mulungu.

¹¹³ Anthu a masiku otsiriza ano amusiya Iye, Mawu owona, Madzi a Moyo; ndipo adzibowolera okha zitsime zachipembedzo; ndipo, kachiwiri, abowola, akumba!

¹¹⁴ Ndipo tsopano ife tikupeza kuti, iwo ali, anali nazo zitsime zong'aluka. Ndiyeno chitsime ichi chadzaza ndi majeremusi a kusakhulupirira, kusakhulupirira kwa kunyada, madongosolo a maphunziro, ndi zina zotero, zomwe ziri zosiyana ndi malonjezo a Mulungu. Iwo ali okaikira a Mawu.

¹¹⁵ Tsopano, zitsime izi zomwe iwo ali nazo, Baibulo linati, zinali “zong'aluka.” Chitsime *Chong'aluka* ndi chitsime “chowukha”, ndipo icho chikuthonya. Kodi icho chikuchita chiyani? Ichu chikuwukhira mu dziwe lazonyansa la zachipembedzo lotchedwa Mgwirizano wa Mipingo ya m'Dzika. Ndipo ndiko kumene chitsime chong'aluka chikuwatsogolera iwo kukalowako, zonse chifukwa iwo amukana Iye, ndipo ali nawo. . . Kasupe wa Madzi amoyo; ndipo apanga zitsime izi.

¹¹⁶ Kukumba madongosolo a seminare yaikulu ya kuphunzira, maphunziro, ndi zina zotero. Ndi mtundu wa zitsime womwe iwo akukumba lero, kuti munthu ayenera kukhala ndi Ph.D., kapena LL.D., kapena Bachala ya Luso, kapena chinachake, iye asanati apite kuti akalalikire. Zitsime zomwe zadzazitsidwa ndi zamulungu zopangidwa ndi anthu. Iwo amazitenga izo kumka mu masukulu aakulu awa a kuphunzira, ndipo mkati mmenemo iwo amabayira mkati mwa iwo zamulungu zawozawo zopangidwa ndi anthu, ndipo amawatumiza iwo kunja ndi zimenezo. Ndi tsiku lotani lomwe ife tiri kukhalamo, zitsime zopangidwa ndi anthu! Palibe vuto ayi. . . Palibe kudabwitsa kuti chinthucho chasandulika—chonunkha, o, mai, ndi chifukwa kuti anthu akumwa kuchokera kwa icho.

¹¹⁷ Ndipo pamene anthu afuna chisangalalo lero, kodi iwo akumachita chiyani? Anthu, mmalo molandira chisangalalo cha Ambuye, iwo akutembenukira ku tchimo, pofuna chisangalalo. Anthu amene amapita ku tchalitchi ndi kumadzinenera

kuti ali antchito a Khristu, pamene iwo akhala amanjenje kwenikweni iwo amayatsa ndudu. Ndipo pamene iwo—pamene iwo afuna kuti—kuti akhale ndi kusangalatsa kwina, iwo amadziphatika zovala zawo zopanda makhalidwe ndi kutuluka ndi kumakatchetcha udzu pamene amuna akuyenda cha pafupi, kuti awafikitse iwo powayimbira iwo muluzi. Iwo amachita chirichonse kuti akhale otchuka. Iwo amafuna kuti aziwoneka monga nyenyezi za pa kanema. Ndicho chisangalalo chawo.

Pamene, Yesu anati, “Ine ndine wowakhutitsa wawo.”

Chifukwa chimene iwo amapitira ku zimenezo, ndi chifukwa iwo samafuna kumamwa kuchokera ku Kasupe ameneyo. Iwo amukana Iye. Iwo sakufuna kumwa kuchokera kwa Iye. Iwo adzijowinitsa okha ku mtundu wina wa kachitidwe kopangidwa ndi anthu, mtundu wina wa chitsime chomwe chiri chodzaza ndi mtundu wonse wa zinthu zachithaphwi, kuti iwo azikhoza kumapita monga chomwecho.

¹¹⁸ Dzulo, ife tinali ndi ana uko ku mtsinje. Ine ndikukhulupirira kuti ilo linali Loweruka mmawa. Ife tinapita kumusi; Billy anali akuweza mu ngalawa. Ndipo ife tinawatengera ana kumtunda, mdzukululu wanga wamwamuna wamng’ono ndi iwo, mwana wanga wamkazi, ndi mwana wanga wamwamuna wamng’ono, ndipo ife tinakwera ndi mtsinjewo kuti—kuti tikakwere ngalawa. Iwe sukanakhoza ngakhale kukwera ngalawa pa mtsinje, chifukwa cha nyansi, zoyipa, anthu auve kunjja uko pa mtsinje, atavala mwatheka ndi kumapitiriza. Ngalawa inayenda pambali pa ife, gulu la aang’ono a khumi ndi ziwiri-, anyamata a usinkhu wa zaka khumi ndi zinayi, aliyense ali ndi chitini cha mowa mu dzanja lake, ndi ndudu. Iwo amakucha iko “kukhala ndi chisangalalo.” O, mai! Dziko ili lingakhoze kutha motalikitsa chotani, ndi kachitidwe kotero monga kameneko?

¹¹⁹ Ndiye kuti adzimasule iwookha kuchokera ku malingaliro akuti iwo akafa adzapita ku gehena, chinthu chomwe iwo amachita, iwo amapita ndi kukajowina chimodzi cha zitsime zopangidwa ndi anthu izi. Kotero mtundu womwewo wa anthu umakhala mu chitsime chimenecho. Sindicho chirichonse koma gulu la osayera, mbululu zauve za mdziko. Ndipo iwo amadziyanjanitsa okha ku izo chifukwa, monga mayi anga achikulire ankakonda kuti, “Mbalame za nthenga zofanana zimawuluka limodzi.” Iwo samati abwere ku Kasupe kuti adzatsukidwe kuchokera ku moyo uwo wa tchimo. Iwo akufuna kuti azikhala kunjja uko, ndi kumagwirizirabe umboni wakuti iwo ndi Akhristu. Chifukwa chiyani? Iwo achoka kwa Iye, Kasupe wona wa chisangalalo, Moyo, Moyo wangwiro ndi chikhutitso. Ndicho chifukwa iwo anachita izo, chifukwa chakuti iwo akufuna kujowinana nazo. Iwo ali nawo mtundu wina wa anthu kumeneko umene umakhulupirira mu zinthu zimenezo.

¹²⁰ Kuno osati kale litali, M'bale Fred ndi ine, ndi M'bale Tom, gulu la ife tinapita ku mpingo wa Baptisti wodziwika mu mzinda wa Tucson, kuti tikawone ngati ife sitikanakhoza kupeza kenakake kakang'ono komwe kakatipatsa ife mwinamwake kumverera kwapang'ono kwa mwatsopano. Ndipo mtumiki ananena chinachake chimzake chokhudza anthu mu Igupto, pamene iwo anachoka iwo anali akudya galiki ndi zina zotero, iwo ankafuna kuti abwerere kachiwiri ndi kukadya izo. Anati, "Ndicho chinachake chonga anthu a lero."

Ndipo, ife, aliyense tinati, "Ameni!" Ine sindinayambe ndawonapo gulu loterolo! Mpingo wonse unasiya kupenya kwa mlaliki ndi kuyang'ana mmbuyo kuti awone yemwe anali amene anati "ameni." Zinakhala ngati ziwawopyseza iwo ku imfa! Iwo sanali kudziwa chomwe icho chinali.

Pamene, Davide anati, "Pangani phokoso lachisangalalo kwa Ambuye. Mtamandeni Iye pa azeze! Mtamandeni Iye ndi malingaka! Mulole chirichonse chomwe chiri nawo mpweya chitamande Ambuye. Ndi zimutamandani inu Ambuye!" Mulungu amasangalala mwa anthu Ake. Asiyeni iwo a ophunzira, anene, "Ameni," pamene chirichonse chanenedwa molondola.

¹²¹ Bwanji osabwerera kuchoka ku kachitidwe aka ndi zitsime za mdziko, kupita ku kachitidwe kokhulupirika ka Mulungu, kamene kali chitsime cha kasupe, Yesu Khristu? Bwanji inu simukutembenukira kwa Iye, kumene Mulungu ali wopereka wathu mochuluka wa chisangalalo, wopereka wathu mochuluka mu matamando, wopereka wathu mochuluka mu kukhutitsidwa? Kutonthola kwa mitsempha yanga kumachokera kwa Mulungu.

Pamene ine ndang'ambidwa, ine ndimapeza kukhutitsidwa kwanga mwa Khristu, osati mu ndudu, osati mu zinthu za m'dziko, osati mu kujowina chikhulupiriro china; koma mu kumupeza Iye, Mawu olonjzedwa amene Iye anati, "Ngati Ine ndipita, Ine ndidzabwerera kachiwiri kuti ndidzakulandireni inu." Ine ndimapeza chisangalalo changa mu zimenezo. Iye ali Chisangalalo changa.

¹²² Iwo amanena lero, pa kujowina zinthu izi ndi pa kupanga Mgwirizano wa Mipingo yonse ya Dziko uwu, kuti iwo akuti apange malo abwino kuti azikhalamo. Mwa kulingalira kwanga kowona mtima, iwo akuti apange malo abwino kuti azichimwiramo. Ndizo basi. . . Chinthu chonsecho ndi tchimo, mulimonse; osati kuti uzikhalamo, koma kuti uferemo. Kupanga malo ake kuti aziseferamo—kuti azichimwiramo, mmalo mwa kukhalamo.

¹²³ Chinthu china chirichonse kunjira kwa Yesu Khristu ndi Mawu Ake a Moyo ndi chitsime chong'aluka. Chirichonse chimene chimayesa kulowetsammalo mwa Iwo; chirichonse

chimene iwe umayesa kuti uchite kuti chikubweretsere iwe mtendere, chirichonse chimene iwe uyesa kuchichita kuti chikubweretsere iwe chithonhozo, mtundu uliwonse wa chisangalalo umene iwe umalandira kuchokera ku chinthu china chirichonse, monga cholowesa mmalo cha Awa, ndi chitsime chong'aluka chodzaza ndi zonyansa. Iye amapereka chikhutitso changwiwo.

¹²⁴ Ine ndikukumbukira kuno, zirimwe zingapo zapitazo, ine ndinatulukira ku khomo lakuseri. Uko kunali shasha wamng'ono kunja uko yemwe ananena kwa ine, anati, "Inu mukudziwa, chifukwa chomwe inu nthawizonse mumayankhula za akazi monga choncho, za kuvala akabudula awo ndi zinthu," iye anati, "chifukwa ndinu munthu wokalamba." Anati, "Ndicho chifukwa chake."

Ine ndinati, "Penya kuno. Ndiwe wausinkhu wanji?"

Anati, "Makumi awiri ndi zisanu ndi ziwiri."

¹²⁵ Ine ndinati, "Pamene ine ndinali zaka zambiri wamng'ono kuposa iwe, ine ndinkalalikira chinthu chomwechi."

Ine ndinapeza Kasupe wa chikhutitso. Iye ali gawo langa. Ameni! Malingana ngati Iye akupereka izo, ndiko kukongola. Ndiko—ndiko kwanga. . . Ndilo luso langa, kuyang'ana pa Iye, kupenya ntchito ya dzanja Lake ndi kuwona zomwe Iye ali kuchita. Palibe kasupe wina yemwe ine ndimamudziwa!

O, kofunika ndiko kusefukira
Kumene kumandipangitsa ine kuyera monga
chisanu;
Palibe kasupe wina ine ndimamudziwa,
Palibe china koma Magazi a Yesu.

Alipo Kasupe wodzazidwa ndi Magazi,
Otengedwa kuchokera mu mitsempha ya
Emanuele,
Mmene ochimwa agwera pansu pa
kusefukirako,
Amataya banga lonse la kuchimwa kwawo.

¹²⁶ Ine ndikukuuzani inu, palibe kasupe wina yemwe ine ndikumudziwa koma Kasupe ameneyo. Iye ananditsuka ine pamene ine ndinali wadokodoko. Iye amandisunga ine wotsukidwa, chifukwa ine ndimafuna kukhala pafupi pomwe pa Iye, kumwa Madzi atsopano awa amene amadzazitsa moyo wanga ndi chisangalalo.

Ine ndikhoza kukhala nthawizonse pansu, ndi kumverera kuti ine sindingakhoze nkomwe kupitako. . .kuzungulira kwinsano, sindingakhoze kupita kwina kulikonse; ndiye ine ndikhoza kugwada pansu ndi kuyika chala changa pa lonjezo, ndi kunena, "Ambuye Mulungu, Inu ndinu mphamvu yanga. Inu ndinu chikhutitso changa. Inu muli zonse-mu-zonse wanga."

Ine ndikhoza kuyamba kumverera Chinachake chikububulikira mmwamba kuchokera mkati mwa ine pamenepo. Ine ndabwera kuchokera kwa icho.

¹²⁷ Monga ine ndadutsa usinkhu wa zaka makumi asanu, ine ndimakhoza kuwuka mmawa, inu mukudziwa momwe izo ziliri, iwe sungathe kupondetsa nkomwe phazi limodzi ilo kuchokera pa kama. Mai, iwe sungakhoze konse kuchita izo; ndipo winawake pa khomo, akugogoda, kapena Billy akundiwuza ine kuti pali chofunika, kwina kwake kumene ine ndiyenera kupitako. Ndipo ine ndimaganiza, “Ine ndingakhoze motani kuchita izo?” Kuyesera kuti ndipondetse phazi limodzi.

Ine ndimaganiza, “Ndinu Kasupe wodzaza ndi mphamvu yanga. Ameni! Mphamvu yanga ndi thandizo langa zimabwera kuchokera kwa Ambuye. Ndinu chitsime changa cha kasupe! Ndinu unyamata wanga! ‘Two amene ayembekezera pa Ambuye adzalimbikitsa mphamvu zawo; iwo adzakwera mmwamba ndi mapingo monga mphungu; iwo adzathamanga, ndipo osakhala otopa; iwo adzayenda, ndipo osakomoka.’ Ambuye Mulungu, iyi ndiyo ntchito yanga, kuti ndipiteko. Ine ndikuyitanidwira ku malo a ntchito.” Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, Chinachake chimayamba kugundagunda mkati mwa ine.

¹²⁸ Tsiku lina, ku malo aang’ono, ine ndinali kuchititsa msonkhano cha kuno mu Topeka, Kansas; uko kunali mnyamata, mlaliki wamng’ono, mmodzi wa othandizira anga oyamba. M’bale Roy, wakhala pano, akuwakumbukira malowo. Mkati umu, mu malo akulu awa uko, uko kunali a—a. . . Mtumiki uyu anali ali pansu pa denga kapena malo, khoma la mmbali linamuperera iye pansu pa ilo. Munthu wamng’ono anali woti afa. Chiwindi chake chinali chitaphulika. Ntchofu yake inali itachoka mmalo ake. Matani atagwera pa iye.

¹²⁹ Ine ndinakhala pa kadzutsa, ndikuyankhula kwa mkazi wanga. Ine ndinati, “Mkazi wanga, iwe ukudziwa, ngati Yesu akanakhala pano, iwe ukudziwa chimene Iye akanachita?” Ine ndinati, “Pamene iye anandithandizira ine, ‘Ine ndikukhulupirira Mawu ajawa,’ iye anali akuthandizira Khristu.” Ndipo ine ndinati, “Iyo ndi ndale ya mdierekezi.” Ine ndinati, “Ngati Yesu akanakhala pano, Iye akanapita kukayika manja Ake oyera pa iye. Mnyamata uyo akanakhala bwino. Ine ndiribe nazo kanthu kuti chiwindi chake chaphulika. Iye akanakhala bwino, chifukwa Yesu akanayenda kulowa mmenemo akudziwa chimodzimodzi Yemwe Iye ali. Iye ankadziwa kuyitanidwa Kwake, Malemba anali kulondola, akutsimikizira mwa Iye kuti Iye ankadziwa Yemwe Iye anali, ndipo osati. . . mopanda mthunzi wa kukayikira. Iye akanayika manja Ake pa iye, ndi kunena, ‘Mwananga, khala bwino,’ kuyenda mochoka pamenepo.” Ndipo ine ndinati, “Kulibe adierekezi okwanira mu gehena akanamupha mnyamata ameneyo, ndiye.” Ine ndinati, “Iye akanakhala bwino.” Koma

ine ndinati, “Iwe ukuwona, wokonedwa, Iye anali Yesu, manja oyera a Mulungu.”

Ine ndinati, “Ine ndine wochimwa. Ine ndinabalidwa kubadwa kwakugonana. Bambo anga ndi amayi onse anali ochimwa, ndipo ndine basi osati-wabwino kalikonse.”

Ndipo ine ndinati, “Koma iwe ukudziwa chiyani? Ngati Ambuye akanandipatsa ine masomphenya ndi kunditumiza ine ndipite uko, ndiye izo zikanakhala zosiyana.” Ine ndinati, “Ine ndikanapita uko ndi kukayika manja anga pa iye, iye akanachoka pa kama ameneyo ngati Iye atandipatsa ine masomphenya.”

¹³⁰ Ndiye ine ndinayamba kuganiza, “Pambuyo pa zonsezo, ngati iwo akanakhala masomphenya, anali chiyani iwo? Iwo akanakhala manja akuda omwewo pa iye, u-nhu, munthu yemweyo akumupempherera iye, manja akuda omwewo.”

Ndiye ine ndinayamba kulingalira, “Ine ndine womuyimirira Wake. Ndiye, Mulungu samandiwona ine. Magazi awo a Mmodzi wolungama uyo ali mmwamba umo pa guwa; iwo amandipangira ine chitetezero. Iye ali wokwaniritsa wanga. Iye ndiye pemphero langa. Iye ndiye Moyo wanga.” Ine ndinati, “Chinthu chokha chimene chingandipange ine kuyika manja anga pa iye, ndi chikhulupiriro, ndi chifukwa chakuti ine ndinali ndi chikhulupiriro mu masomphenyawo. Ndipo popanda masomphenya, chikhulupiriro chomwecho chingachite chinthu chomwecho; kotero ine ndikhoza kudziwerengera ndekha osati kanthu, koma kumuwerengera Iye zonse-mu-zonse wanga. Iye ali Moyo wanga. Iye ali Kazembe wanga. Palibe chipembedzo chimene chinadituma ine; Iye anadituma ine. Aleluya! Ine ndikupita mu Dzina Lake. Ine ndikayika manja pa iye.” Ndinayenda kupita kumeneko ndi kukasanjika manja pa mnyamata ameneyo, ndipo usiku umenewo iye anali mu msonkhano, wabwino molimba. Amen!

¹³¹ O, inde, Iye ndiye Kasupe ameneyo. “Palibe kasupe wina yemwe ine ndikumudziwa. Palibe china koma Magazi a Yesu!” Ine ndine wonunkha, ine ndine chigawenga, mmodzi aliyense wa ife tiri, koma pamaso pa Mulungu ife tiri angwiro. Ye-. . . “Khalani inu chotero angwiro, ngakhale monga Atate anu Kumwamba ali angwiro.” Inu mungakhoze kukhala chotani? Chifukwa Mmodzi wangwiroyo akutiyimira ife kumeneko. Kasupe ameneyo ali kumeneko tsiku lililonse, ozizira. Osati chithaphwi chinachake, koma watsopano tsiku lililonse, yemwe amatsuka machimo anga onse. Iye ndiye Kasupe ameneyo.

¹³² Tsopano mu kutseka, ine ndikhoza kunena izi. Chirichonse chosiyana kwa Uyu ndi zitsime zong’aluka, ndipo potsiriza zidzaukhitsa zomwe inu mwayika mu izo; ngati inu mukuyikamo ziyembekezero zanu zonse, nthawi yanu yonse, ndi chirichonse, mu chimodzi cha zitsime zazithaphwi izo. Yesu anati izo zinali

zitsime zong'aluka. Mulungu anati, "Izo ndi zong'aluka, ndipo izo zidzaukhitsa zonse zomwe inu mwayika mu izo." Inu simungakhoze kupita patali paliponse ndi izo, chifukwa izo ziwukhamo. Pakuti Iye ali njira yokha yopitira ku Choonadi, ku Moyo, ndi ku chisangalalo Chamuyaya, ndi mtendere Wamuyaya. Iye ali Mmodzi yekha ndi njira yokha kwa Izo. O, mai!

¹³³ Kasupe wosaguga wa Moyo ndi Yesu Khristu. Chifukwa chiyani? Ndipo kodi Iye ndi Ndani? Mawu, yemweyo; Mawu, Moyo, Kasupe, "yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse." Wokhulupirira woona, Ndi chisangalalo chake chapamwamba, Moyo wake wapamwamba. Ndipo chikhutitso chake chapamwamba chiri mwa Khristu. Mopanda kupompa, mopanda kukoka, mopanda kujowina, mopanda kulipira; kungokhulupirira ndi kupumula. Ndicho chomwe Iye ali kwa okhulupirira.

¹³⁴ Monga atate Abrahamu; iye sanakoke konse, iye sanawope konse, iye sanadandaule konse. Iye anali nawo Mawu. Iye ankagona pa bere la El Shaddai. Pamene Abrahamu anali usinkhu wa zaka zana, Mulungu anawonekera kwa iye, ndipo anati, "Ine ndine Wamphamvuzonse." Mawu Achihebri ndi *El Shaddai*, kutanthauza, "Mmodzi-Wamabere." "Ndipo iwe ndi wokalamba, ndipo mphamvu yako yapita, koma ingogona pa chifuwa Changa ndipo yamwira mphamvu yako kuchokera ku Kasupe uyu." Amen! Kodi iye anadziyamwira yekha ku chiyani? Thupi latsopano. Iye anali naye mwana, mwa Sarah. Ndipo, zaka makumi asanu mtsogolo, anali ndi ana asanu ndi awiri mwa mkazi wina.

¹³⁵ O, El Shaddai! Chipangano Chakale chimasonyeza zomwe Iye anachita, Chipangano Chatsopano chikunena zomwe Iye ati adzachite. Amen! Mu Chipangano Chakale . . .

¹³⁶ Tsopano mpweya watha, kotero ine ndifulumira ndi kusiyira pano tsopano, mu miniti chabe.

Ine ndikufuna kunena izi ine ndisanatseke. Ine ndinali nacho chitsanzo chabwino cha nthawi imodzi iyi. Ine ndinali kulondera. Ndipo anthu ambiri kuno . . . Kumusi kuzungulira Georgetown, kumusi uko mu Milltown, kumeneko kunali, kutali komwe mu mapiri, kasupe. Icho chinali chitsime cha kasupe. Icho chinkalavula pafupi i—inayi—kapena mtsinje wa nthambi zisanu za madzi, kumangokhuthukira kunja nthawi zonse, ndipo kasupe wamkulu kwambiri kuzungulira kumeneko. Ndipo kuzungulira kumeneko kunali zochuluka za zitsamba izi kuno, inu mukudziwa, ndi zinthu zikumera pamenepo, zomwe zonga-minti. Ndipo, o, ine ndinali kumamva ludzu ndikafika kumeneko, o, mai, kuti ndikafike ku kasupe ameneyo. Ndipo ine ndimakhoza kugona pansu pa chinthu ichi ndi kumangomwa ndi kumwa, ndi kukhala pansu ndi kumwa, kuyembekezera.

Ndipo chaka ndi chaka ine ndimabwera basi ku kasupe yemweyu. Iye sanali kuleka konse, dzinja kapena chirimwe. Iwo samakhoza kumuwumitsa iye. Inu simungakhoze kuwumitsa chitsime cha kasupe. O, ayi! O, ayi! Ine sindikusamala motani—kaya kukhala kozizira chotani, iko sikumuwumitsa iye. Inu mukhoza kuwumitsa chitsime; chisanu pang’ono chokha chikhoza kuchita zimenezo. Mwaona?

Koma chirichonse chimene chikusuntha, chiri ndi Moyo mwa icho, chiri kusuntha pozungulira. Ndipo inu simungakhoze kuwumitsa chitsime cha Kasupe. Ziribe kanthu momwe mzimu uli wopsyinjika pozungulira malowo, Kasupe uyu nthawizonse ndi wamoyo. Khalani pa Kasupe ameneyo.

¹³⁷ Ndipo ine ndinazindikira pamenepo, ine ndinkapita pamenepo ndipo ndimamwa pa iye, ndipo, o, mai, madzi ozizira basi! Iwe sumasowa kuti uzidandaula, “Ndikudabwa, ngati ine ndikakafika pamenepo, ndikudabwa ngati iye ati asiye kuyenda?” Iye wakhala akuyenda. . .

¹³⁸ Mchikumbe wachikulire anandiuza ine, anati, “Agogo anga aamuna ankanwa kuchokera kwa iye.” Ndipo anati, “Iye sikuti anathapo kapena kalikonse. Iye akanali chitsime chomwecho, akutumphukira kupita mu Mtsinje wa Buluu kumeneko.”

¹³⁹ Ine ndinaganiza, “O, mai, ndi malo abwino bwanji kuti ukamweko!” Ine ndimakhoza kuyenda pafupi mailo kuchoka mu njira, kuti ndikafike ku malo amenewo, chifukwa iwo anali malo enieni chotero kuti ukamwepo. O, anali abwino bwanji madzi amenewo! O, mai!

Ine ndima—ine ndimafika kunja uko mu chipululu icho, Arizona tsopano, ine ndinali ndikuganizabe za iye, “Chitsime chodabwitsa chimenecho kumusi kumeneko, ngati ine ndikanati ndikangogona pansu pamenepo!”

Monga Davide ananena nthawi yina, “O, ngati ine ndikanakhoza kamodzi kenanso kumwa kuchokera ku kasupe ameneyo!” Ngati iye akanati angokafika kumeneko!

¹⁴⁰ Ndipo ine ndinakhala pansu tsiku lina, ndipo ine ndinali ndi kanthu kakang’ono koseketsa kamene kanachitika kwa ine. Ndipo ine ndinati, “Nchiyani chimene chimakupangitsa iwe kukondwa chotero nthawi zonse? Ine ndikukhumba ndikanakhala ndiri wokondwa monga choncho. Bwanji, ine sindinakuwonapo iwe utakwiya, chiyambire ine kubwera kuno. Palibe kanthu kamodzi kachisoni za iwe.” Ine ndinati, “Iwe nthawizonse ndi wodzaza ndi chisangalalo. Iwe ukulumpha ndi kububulika ndi kumapitiriza. Dzinja kapena chirimwe, kuzizire kapena kutenthe, chirichonse chomwe chiri, iwe nthawizonse ndiwe wodzaza ndi chisangalalo. Nchiyani chomwe chimakupangitsa iwe. . . ? Chiyani, nchiyani icho? Chifukwa ine ndimamwa kuchokera pa iwe?”

“Ayi.”

Ine ndikuti, “Chabwino, mwinamwake akalulu amamwa kuchokera mwa iwe, ndipo iwe umakonda zimenezo mochuluka kwambiri.”

“Ayi.”

Ine ndinati, “Chabwino nchiyani chimakupangitsa iwe kububulika monga choncho? Nchiyani chimakupangitsa iwe kukondwa chotero? Nchiyani chimakupangitsa iwe nthawizonse wodzaza ndi chisangalalo?” Ndinati, “Kodi ndi chifukwa kuti—kuti mbalame zimamwa kuchokera pa iwe?”

“Ayi.”

“Chifukwa ine ndimamwa kuchokera pa iwe?”

“Ayi.”

Ine ndinati, “Chabwino, nchiyani chimakupangitsa iwe kukhala wodzaza chotero ndi chisangalalo?”

¹⁴¹ Ndipo ngati kasupe ameneyo akanakhoza kuyankhula mobweza kwa ine, iye akananena izi. “M’bale Branham, osati chifukwa inu mumamwa; ine ndikuyamikira zimenezo, ndipo chifukwa kuti ine ndimasamalira mbalame. Ine ndimasamalira aliyense yemwe akufuna kumwa. Chinthu chokha chimene inu muyenera kuchita ndi kubwera pano ndi kudzamwa. Koma, chomwe chimandipangitsa ine kukondwa, si ineyo yemwe ndikububulika, ndi chinachake mkatimu, chikundikankha ine. Ndicho chinachake chikundibubulitsa ine.”

¹⁴² Ndipo ndimo momwe ziriri ndi moyo wodzazidwa ndi Mzimu. Monga Yesu ananena, Iye anali mu...Onani, Iye akupatsani inu zitsime za madzi otumphukira ku Moyo wosatha, chitsime cha kasupe, madzi ambiri osekukira omwe akuyenda mowirikiza. Kaya mpingo wonse uli mmwamba kapena pansu, iwe ukadali pa Kasupe ameneyo.

Inu mukanatenga chifukwa chiyani kachitidwe kachikale ka chipembedzo ndi chitsime, chodzaza tizirombo ndi chinthu chirichonse, ndi kumamwa pa chinthu chachithaphwi icho, pamene inu mwayitanidwira ku Kasupe, chitsime cha Kasupe?

¹⁴³ Ine ndikuganiza momwe iye amangokhala akukankha, ndi kujowa, ndi—ndi kugugulika, ndi kuseka, ndi kusangalala, ndi kukondwerera, ndi kunyan’gwa. Kuzizire, kukhale mvula; kutenthe, kuwume, pamene dziko lonse linali kumawuma, iye anali kububulika basi monga iye amachitira nthawizonse. Chifukwa iye anali wakuya, wozikika, pansu penipeni mu miyala iye amatulukira.

¹⁴⁴ O, ndiroleni ine ndizikhala cha pa madzi okhuthukawo! Tengani machitidwe anu onse opangidwa ndi anthu omwe inu mukuwafuna, mipope yanu yonse yazithaphwi, koma ndiroleni ine ndibwere ku...kapena zitsime za zithaphwi. Koma, ndiroleni ine ndibwere ku Kasupe uyu, ndiroleni ine ndibwere kumeneko komwe iye ali wodzaza basi. Iye ndiye

chisangalalo changa. Iye ndiye Kuwala kwanga. Iye ndi wanga— Iye ndiye Nyonga yanga. Iye ndiye Madzi anga. Iye ndiye Moyo wanga. Iye ndiye Mchiritsi wanga. Iye ndiye Mpulumutsi wanga. Iye ndiye Mfumu yanga. Chirichonse chimene ine ndiri kuchisowa chiri kupezeka mwa Iye. Ine ndikanafunira chiyani kuti ndipite ku china chirichonsenso?

¹⁴⁵ M'bale, mlongo, kodi inu simubwera ku Kasupe ameneyu usikuuno? Simutero inu, ngati inu simunayambe mwakhalapo konse kumeneko, kodi inu simumulandira Iye usikuuno pamene ife tikuweramitsa mitu yathu?

¹⁴⁶ Zitsime zong'aluka, zowukha, zotayikira, dziko kutayikira mu izo, nyansi zochokera ku mabarani ndi za masiku ena. Bwanji osati Chitsime ichi, zinthu zimenezo sizingakhoze kukhala mmenemo, Kasupe wamkulu uyu wodzaza ndi Magazi, otungidwa kuchokera ku misempha ya Emanuele? Bwanji inu simukuwalandira amenewo usikuuno? Mulungu atatithandiza ife usikuuno, mu dziko lowuma ili, laludzu. Monga mneri anati, "Iye ndiye Thanthwe mu dziko lotopetsa." Iye ndiye Kasupe ameneyo. Kodi inu simuti mubwere kwa Iye usikuuno, mu mitima yanu, pamene ife tikupemphera?

¹⁴⁷ Wokonedwa Atate Akumwamba, palibe Kasupe wina, monga nyimbo ikusewerera, "Palibe kasupe wina yemwe ine ndikumudziwa; palibe china koma Magazi a Yesu." Ine ndinabadwira mmenemo, ine ndakhala ndikuleredwera mmenemo; ine ndikufuna ndizikhala mmenemo, ndi kufera mmenemo, ndi kudzawukanso mmenemo, mu Kukhalapo Kwake. Nthawizonse, Ambuye, ndiroleni inu ndizikhala mu Kukhalapo Kwake, pakuti palibe wina yemwe ine ndikumudziwa. Palibe chikhulupiriro, palibe chikondi; palibe chikondi koma Khristu, palibe chikhulupiriro koma Khristu, palibe bukhu koma Baibulo, palibe chinthu chirichonse, palibe chisangalalo kunja kwa Iye. Mukamuchotsa Iye kwa ine, O Mulungu, ine sindikusamala kuchuluka kwa za dziko zomwe ine ndinali nazo, izo—izo zikanakhalabe zakufa, ine ndikanamayendayenda chozungulira ndi manja anga mwamba pa mutu wanga. Mukamuchotsa Iye kwa ine, ine ndikhala nditapita, Ambuye. Koma msiyeni Iye akhale mwa ine, ndiye Disembala akhala wokoma monga Meyi, ndiye sipakhala malo otentha ndipo sipakhala malo owuma, ngakhale imfa iyoyomwe ilibe chigonjetso. Tiroleni ife tikhale naye Iye, Atate. Mperekeni Iye, mwa kuchuluka, kwa wokhulupirira aliyense pano usikuuno, pamene iwo ayembekezera mu chipinda chino.

¹⁴⁸ Ambiri a iwo ayenera kuyendetsa molondola msewu usikuuno, pamene iwo azipita ku nyumba zawo, ndipo ichi chitakhala choganiza chawo, "Ine ndikukhala pa Kasupe ameneyo. Ine ndikukhala pamene, kumwa mwatsopano, ora ndi ora."

149 Ndipo ngati iwo sanalandire icho, panobe, mulole iwo amulandire Iye tsopano, kotero iwo akhoza kumutenga Kasupe uyo limodzi nawo. “Ine ndipita ndi inu; ine ndidzakhala ndi inu mpaka kumathero a dziko.” Perekani zinthu izi, Atate.

150 Ndipo tsopano pamene ife tiri ndi mitu yathu itaweramitsidwa, kodi alipo winawake muno, usikuuno, kapena ndi angati amene akanati, “Ambuye, nditengereni ine ku Kasupe ameneyo pakali pano. Ine sindinabwere muno kudzangomva; ine ndabwera muno kuti ndidzafufuze Chinachake. Ine ndabwera muno kuti ndidzakupezeni Inu, Ambuye. Ine ndiri nako kusowa kwa Inu usikuuno. Bwerani ku mtima wanga pakali pano. Kodi inu mungachite izo, Ambuye?” Mulungu akudalitseni inu. Ambuye adalitse wina aliyense.

151 Atate, Inu mwawona manja, ngakhale mmwamba ndi pozungulira khoma, ndi muzipinda zinazo, kunja. Inu—Inu mwawawona iwo, Atate. Ine—ine ndikupemphera kuti Inu mupereka chirichonse chomwe iwo ali kuchisowa. Mwinamwake iwo akhala akumwa pa chitsime china chakale, Ambuye, kungokhala kuyima kwa theka laulendo pamene munthu wina anabowola chitsime, icho chakhala chithaphwi ndi mitundu yonse ya ziphunzitso zachirendo, kuwakana Mawu. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti usikuuno iwo abwere kwa Iye Yemwe ali Kasupe uja, Kasupe wa Moyo ameneyo. Perekani izo, Atate. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu tsopano mu Dzina la Yesu.

152 Ndipo Inu munandiwuza ine, “Ngati iwe upempha chirichonse mu Dzina Langa, icho chidzachtidwa.” Tsopano, ine sindikanapempha izi, Ambuye, ngati ine ndikanati ndisaganize kuti izo zikanachitidwa. Ine ndikanakhala—ine ndikanakhala ndikungonena izo mwa chizolowezi cha mwambo. Koma ine ndikuwapempherera iwo, ndi kuwona mtima. Ine ndikuwapempherera iwo, ndikukhulupirira kuti Inu mupereka zimene Inu munalonjeza.

153 Ndipo tsopano ine ndikuwachotsako iwo atalikire ndi chitsime chimenecho usikuuno. Ine ndikuwachotsako iwo atalikire ndi malo omwe iwo akhala akumwako, kumene iwo sanali akukhutsidwa; kubwera ku Kasupe uyu. Ine ndikuchita izo mu Dzina la Yesu Khristu.

154 Iwo ali Anu, Ambuye. Aloleni iwo amwe kuchokera kwa Inu, Madzi Amoyo, Kasupe wa Madzi amoyo. Mu Dzina la Yesu, ine ndikupempha izi. Amen. Perekani izo, Ambuye.

O, kofunika ndi kuyendererako
Kumandiyeretsa ine monga chipale;
Palibe kasupe wina ndimdziwa,
Kupatula Magazi a Yesu.

Nchiyani chingatsuke tchimo langa?
 Kupatula Magazi a Yesu;
 Nchiyani chingandipange wamphumphu
 kachiwiri?
 Kupatula Magazi a Yesu.

O Yesu, achizeni awa, Ambuye! Perekani izo, Ambuye, kupyolera mu Dzina la Yesu. Ine ndikupemphera, Mulungu kuti Inu . . . ? . . . Inu mumadziwa zinthu zonse.

Palibe kasupe wina ndimdziwa,
 O, kupatula Magazi a . . .

¹⁵⁵ Taganizani za izo, palibe kasupe wina yemwe ine ndikumudziwa! Ine sindikudziwa kanthu kena kalikonse kupatula Iye. Ine sindikukhumba kuti ndidziwe kanthu kena kalikonse kupatula Iye. Palibe china kupatula Magazi a Yesu! O!

O, kofunika ndi kuyendererako
 Kumandiyeretsa ine monga chipale;
 Palibe kasupe wina ndimdziwa,
 O, kupatula Magazi a Yesu.

¹⁵⁶ Pamene ife tikuyimba iyo kachiwiri, tiyeni tigwirane chanza wina ndi mzake. Kodi inu mumakondana wina ndi mzake? Kodi alipo winawake muno yemwe ali ndi chirichonse chotsutsa wina aliyense? Ngati alipo, pitani mukachikonze icho. Kodi inu mutero? Tiyeni tisachoke pano monga choncho. Mwaona? Ngati inu muli ndi mangawa motsutsa winawake, inu mupite mukachikonze icho, pakali pano. Pakali pano ndi mwayi wanu kuti mupite, kukati, “M’bale, mlongo, ine ndinanena chinachake za inu, ine ndimaganiza chinachake. Ine sindimatanthauza kuchita icho. Ndikhululukireni ine.” Mwaona, ndimo momwe ungachitire izo. Tiyeni tikhale naye Kasupe pakati pathu pomwe, nthawi zonse. Mwaona?

Palibe kasupe wina ndimdziwa,
 Kupatula Magazi a Yesu.
 O, kofunika ndi kuyendererako
 Kumandiyeretsa monga chipale;
 O, palibe kasupe wina ndimdziwa,
 Kupatula Magazi a Yesu.

¹⁵⁷ O, kodi Iye sali wodabwitsa? Palibe kasupe wina! Ife sitidziyipitsa tokha ndi zinthu zina. Ife tapatula, talisiya dziko mmbuyo. Ife sitikufunanso galiki wa ku Igupto ndi zitsime zong’aluka. Ife tiri mu ulendo ndi Ambuye Yesu, Thanthwe lokanthidwa lija, ameni, kudya Manna ochokera Kumwamba, ndi kumwa; kudya Chakudya cha angelo, ndi kumwa kuchokera ku Thanthwe. Ameni!

Palibe kasupe wina ndimdziwa,
 Kupatula Magazi a Yesu.

Tsopano tiyeni ife tiweramitse mitu yathu.

158 Kupemphera kuti Mulungu akudalitseni molemerera aliyense wa inu, kuti chisomo Chake ndi chifundo zikhale ndi inu kupyola mu sabata likudzali. Ndipo ngati chirichonse chikati chichitike, kuti mmodzi wa inu angazembere kupyola chotchinga tsopano, ingokumbukirani kuti ndi maora pang'ono okha ogona ndi kupumula mpaka pomwe tidzawonane. Kumbukirani, kuti, "Iwo amene ali moyo natsala sadzalepheretsa iwo amene ali kugona, pakuti Lipenga la Mulungu, Lipenga lotsiriza lija. . ." Lachisanu ndi chimodzi langowomba kumene. Ndipo Lipenga lotsiriza ilo, munga Chisindikizo chotsiriza, lidzakhala kuli Kudza kwa Ambuye. "Ilo lidzawomba, ndipo akufa mwa Khristu adzawuka poyamba." Akungomapumula mpaka nthawi imeneyo.

159 Ndipo ngati inu muti muvulazidwe, kumbukirani:

Tengani Dzina la Yesu limodzi ndi inu,
Monga chishango ku msampha uliwonse;
Ndipo pamene mayesero asonkhana
pozungulira inu,
Ingopumani Dzina loyera ilo mu pemphero.
(Ziwanda zidzathawa.)

160 Ingokumbukirani, ife tikuyembekeza kuti tikomana nanu inu pano Lamlungu lotsatira mmawa. Dzabweretseni muno odwala ndi osautsika. Ine ndidzakhala ndiri kukupemphererani inu. Inu mundipempherere ine tsopano. Kodi inu mutero? Nenani, "Ameni." [Osonkhana, "Ameni."—Mkonzi.] Ine ndikupemphererani inu, kuti Mulungu akudalitseni.

. . . Dzina mu pemphero.

Dzina lofunika, Dzina lofunika, O kukoma kwake!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba;

Dzina lofunika, O kukoma kwake!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba

Pa Dzina la Yesu kuwerama,
Kudzigwetsera pa mapazi Ake,
Mfumu ya mafumu Kumwamba ife
tidzamuveka Iye korona,
Ulendo wathu ukadzatha.

Dzina lofunika, Dzina lofunika, (kodi ilo si lokoma ndi lofunika?)

Chiyembekezo cha pa dziko ndi chimwemwe cha Kumwamba;

Dzina lofunika, Dzina lofunika, O kukoma kwake!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba.

¹⁶¹ Ndi nthawizonse chovuta kwambiri kuti ndikusiyeni inu. Ngakhale ine ndikudziwa inu mukutenthedwa, koma pali chinthu chinachake basi za... Tiyeni, ndime imodzi inanso ya chinachake, kodi inu muchita izo? [Osonkhana, "Ameni."—Mkonzi.] Kodi muchita izo? *Chodala Chikhale Chimango Chomwe Chimamangiriza*, mlongo. Ndi angati amayidziwa nyimbo yakaleyo? Ife tinkakonda kuyiyimba iyo, zaka zapitazo.

¹⁶² Ndipo ine ndinali kuganiza, usikuuno, "manja awiri, kuchokera pa mazana, omwe atsalira," pamene ife tinkakonda kuyimba nyimbo imeneyo pa kachisiyu, ndi kulumikizana ndi dzanja la wina ndi mzako. *Chodala Chikhale Chimango Chomwe Chimamangiriza*. Ine ndakwirira ochuluka a iwo, apa pomwe pamanda. Iwo akuyembekezera. Ine ndidzawawona iwo kachiwiri. Ine ndimawawona iwo, kamodzi mwa kanthawi, mu masomphenya, pamene ine ndiyang'ana kuseri kwa chotchinga. Iwo ali kumeneko.


Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano pamene ife tikuyimba.

Chodala chikhale chimango chimatimangiriza
Mitima yathu mu chikondi cha Chikhristu;
Chiyanjano . . .
Chiri chonga chiya Chakumwamba.

Pamene ife . . . (tsopano fikirani ndi kugwira
dzanja la winawake) . . . tisiyana,

Tsopano weramitsani mutu wanu.

Chimatipatsa ife kupweteka mkati;
Koma tidzakhalabe olumikizana mu mtima,
Ndi kuyembekeza kudzakomananso.

¹⁶³ Ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ine ndikutembenezira msonkhano kwa abusa tsopano, ndipo atibalalitse mu . . . 

ZITSIME ZONG'ALUKA CHA64-0726E
(Broken Cisterns)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingerezi pa Lamlungu usiku, pa Julaye 26, 1964, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1996 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1996 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org